

# KUKOPA KWA WINA



Zikomo inu, M'bale Neville. Ambuye akudalitseni inu.

Usiku wabwino, abwenzi, chiri chabwino kwambiri kukhala ndiri pano kachiwiri usikuuno pa kachisi, kuti tidzayankhule kanonso za Ambuye wathu ndi Mpulumutsi, Yemwe ife tonse tiri mu chikondi naye ine ndikutsimikiza, kapena ife sibwezi titakhala pano mu nyumba yotentha ino, titapanikizana momwe ife tiriri usikuuno, ngati ife tikanati tisamamukonde Iye. Chifukwa ndicho cholinga chathu cha kukhala pano, ndi kuti tidzafotokozere kwa Iye kuti ife timamukonda Iye. Ndipo ziyembekezere zathu ziri—zimasunthidwa kwakukulu pamene ife tiganiza za kuyandikira kwa nthawi Yake. Pamene ife tikuwona zizindikiro zikuwonekera za kudza Kwake, ife tikuyembekezera ora lalikulu limenelo pamene ife titi tidzamuwone Iye.

<sup>2</sup> Chikhalireni kuno Lamlungu la sabata lapitalo, pakhala pali ambiri omwe apita kuti akakomane naye Iye. Mmodzi anali Akazi a Ford, Akazi a Levi Ford. Iwo anali usinkhu wa zaka makumi asanu ndi atatu, mzimayi wofunika. Amuna awo anamwalira nthawi yina pakale. Iye anali msirikali wakale wa Nkhondo ya Aspanishi ndi Amereka. Ndipo mu mbiri ya moyo wanga ine ndinatchula dzina la mwana wawo. Iye anali mmodzi yemwe anali woti andipatse ine suti ija, inu mukudziwa, iye atatha kuyivala iyo mokwanira, ijayi—suti ya—ine ndikukhulupirira iyo inali suti ya mnyamata wolondolera. Ndipo iye. . . Pamene ine ndinapita kuti ndikatenge gawo la iyo, uko kunali mwendo umodzi wokha utatsalira mu iyo.

<sup>3</sup> Lloyd mwinamwake ali pano usikuuno, mnyamata yemweyo. Ndipo ine—ine ndinali ndi maliro a amayi ake tsiku lina. Ndipo iye anandifunsa ine, anati, “Billy, ine ndikukhumba iwe ukanayankhula pa chinachake chimene chikutsimikizira kuti amayi anga adzawuka kachiwiri.” Ndipo Ambuye anandipatsa ine uthenga wa izo pa cholondola, chenicheni. . . Pamene Baibulo, chirengedwe chonse, chirichonse chimene Mulungu anachirenga chikuyankhula izo, iye adzawuka kachiwiri. Ndani—ndani yemwe ati ayankhule motsutsa icho ndiye? Mulungu akunena chomwecho, akutsimikizira icho mwa chirengedwe Chake, akutsimikizira icho mwa Mawu Ake, akutsimikizira icho mwa moyo wake, china chirichonse, iye ayenera kudzawuka, inu mukuona. Palibe njira, palibe kalikonse. . . Kumwamba ndi dziko lapansi zikhoza kulephera, koma chimenecho sichingakhoze kulephera. Iye ayenera kudzatulukira kachiwiri.

<sup>4</sup> Ndiye tsiku la dzana, manenjala yemwe anakonda kukhala ndi ine, Bambo Baxter (ambiri a inu mukumukumbukira

iyeye; iyeye anayankhula kuchokera pa nsanja iyi), mkazi wake anafa mwadzidzidzi ndi kuyima kwa mtima. Ndipo iyeye ali wong'ambika kwambiri ndi wachisoni kwambiri; ndipo ine ndikuyembekeza—ndikudalira kuti inu mukamukumbukira M'bale Baxter mu mapemphero anu pamene inu muzikapemphera, chifukwa iyeye ndi mmodzi wa abale athu. Ndipo iyeye amakhala mu Vancouver, British Columbia. Ndipo iyeye sanakhale ali ndi ine tsopano kwa chiwerengero cha zaka. Ndipo ine ndinamva kuti mkazi wake anakhala ngati anali ndi kusokonezeka kwa misempha kapena chinachake, ndiyeno zonse mwadzidzidzi iyeye anatenga kuyima kwa mtima ndipo wapita. Iye sitingadziwe basi nthawi yomwe iyo iti itiyitane. Ndiyeno pamene iyo—Iye ayitana, ife tiyenera kukhala okonzeka. Ndicho chifukwa chomwe ife tiri pano usikuuno.

<sup>5</sup> Ine ndinali mowerengera uko—ofesi, kani, ndimayankhula ndi Bambo Moore. Iwo andikakamiza ine . . . ine ndinali . . . ? . . . ine ndinali kuyesera kuti ndichokepo pa Kuperekamathokozi; ine ndimafuna kuti ndidzakhale ndi msonkhano kuno wa Tsiku la Kuperekamathokozi; ndipo kenako kupita ku Shreveport. Ndithudi, ine—sindikyanati ndikwanitse konse zimenezo. Ndipo potsiriza iyeye anati, “Chabwino, ngati muli—tiri nayo misonkhano itatu tsopano ndipo tikuti tikhale ndi Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri izo kenako, ndiye inu mukanakhoza kutipatsa ife tsiku limodzi limenelo mulimonse.” Chotero potsiriza, ife timati tiwapatse awo Lachisanu, Loweruka, ndi Lamlungu. Ndipo tsopano, ine ndamulonjeza iyeye ndiye Lachinayi, Lachisanu, Loweruka, ndi Lamlungu. Ndipo ilo lidzakhala . . . Pentekoste idzakhala itakwanitsa zaka makumi asanu mu Louisiana—Tsiku la Kuperekamathokozi. Iyo inagwa zaka makumi asanu zapitazo mu Louisiana.

<sup>6</sup> Tsopano, mawa mmawa tati tidzakhale ngati kukakamiza kuti aliyense yemwe alibe—Sande sukulu yomwe muti mukakhaleko . . . Ine ndikumuwona M'bale wathu wofunika Don Ruddell kuno, ndipo ine ndikudziwa iyeye amakhala ndi Sande sukulu mmawa. Ndipo mwinamwake muli atumiki ena muno ochokera kuzungulira koyandikana naye omwe ali nayo Sande sukulu. Tsopano, ife tikufuna inu kuti mupite ku Sande sukulu yanu yanu ngati inu muli nayo iyo. Koma ngati inu mulibe Sande sukulu, ndipo inu mukukonda kuti mukhale ndi ife, ine ndikufuna kuti ndiyankhule mmawa, ndi kutulutsa bolodilakuda, ndi kudzaphunzitsa pa *Thunthu Lamphumphu la Munthu Wangwiro*, ndi kuzijambula izo apo mu—pa bolodilakuda, ndi kusonyeza zofunikira za Mulungu ndi momwe ife tingafikire ku thunthu langwiro la—la munthu wangwiro pamaso pa Mulungu.

<sup>7</sup> Ndiyeno mawa usiku, Ambuye akalola, ine ndikufuna kuyankhula pa phunziro la *Namulondola Wanga*. Chotero ngati ena a inu omwe muli ochokera kunja kwa mzinda . . . Ndipo ife

tikufuna kuti tiyese kuyamba misonkhano imeneyi molawirira ngati...ine sindinayankhule nawo abusa panobe, koma ine ndikukhumba inu mukanayamba Sande sukulu molawirira kwenikweni mmawa. Ndipo mpingo mawa usiku, mwinamwake, ngati nkotheke, kuyambira pa 6:30 kapena chinachake. Ndipo chimenecho chidzawapatsa anthu mwayi kotero ngati iwo akufuna kuti atsale...Ife tikanakhoza kutuluka pofika 8:30, ndiyeno ena a iwo...

<sup>8</sup> Ine ndinakomana naye dona lero yemwe amayendetsa atatu kapena anayi, pafupi...Iye anati, ngati ife titati tituluke 8 koloko kapena 8:30, iye akanati akafike kwawo mma 2:30 kapena 3 koloko mmawa wotsatira, amuna ake akupita ku ntchito...Chotero ife sitikhala tikuchita chirichonse mulimonse koma kumanyenya pozungulira, chotero—chotero tiyeni tingobwerani ku tchalitchi molawirira. Ndipo ife tiribe... Inu mukudziwa, ife sitisowa kukhala nawo mawonekedwe pa izi; Mulungu ndi wopanda mawonekedwe, inu mukudziwa, Baibulo...?...Chotero, ife tikuyembekeza kuti inu muli pano, ndi—onse omwe angakhoze kukhala.

<sup>9</sup> Tsopano, ngati inu muli ndi misonkhano yanu yanu, kumbukirani, uyu ndi kachisi wa zipembezozo zosiyanasiyana kumene anthu...?... amabwera. Ndipo ambiri a unyinjira wathu ali opangidwa kuchokera mwa anthu a kunja-kwa-mzinda.

<sup>10</sup> Tsopano, ngati pachitika kuti pali mlendo pano, ine ndikufuna kuti ndikusonyezeni inu chinachake. Ndipo ine ndangoyenda kubwera ku nsanja ndipo ine sindikuwona—ine sindikuwawona anthu khumi omwe ine ndikuwadziwa. Ndi anthu angati pano ali ochokera kunja kwa mzinda wa Jeffersonville, kwezani dzanja lanu. Mwaona, makumi asanu ndi anayi mphambu asanu ndi anayi pa zana. Mwaona, mukuona? Ndi abwenzi okha. Ndi angati ali muno ochokera ku mtunda wa mailosi zana, kwezani mmwamba dzanja lanu. Alipo makumi asanu pa zana a iwo, ochokera ku mtunda wopitirira mailosi zana. Ndi angati ali muno aku mtunda wopitirira mailosi mazana awiri, kwezani mmwamba dzanja lanu. Mtunda wa mailosi mazana atatu, kwezani mmwamba manja anu. Tayang'anani apo! Mtunda wa mailosi mazana anayi, kwezani mmwamba dzanja lanu. Tayang'anani apa! Mtunda wa mailosi mazana asanu, kwezani mmwamba dzanja lanu. Tayang'anani apo, kupitirira chitatu cha osonkhana akutali kupitirira mtunda wa mailosi mazana asanu! Mwaona, ndi abwenzi okha omwe amasonkhana muno kuchokera kozungulira...?...ife tikhala tiri pano. Kotero ife tiri oyamikira chifukwa cha inu, ndipo ife tiri pano kuti tikuthandizeni inu. Ife tiri pano kuti tichite zonse zimene ife tingakhoze chifukwa cha inu.

<sup>11</sup> Ndipo tsopano, ine ndinali kungowerenga kumbuyo uko ena—kalata imene mwana wanga wangondipatsa ine ya dona yemwe akuti iyi—kubwera nthawi ino akhala maulendo makumi

atatu ndi kasanu omwe iye wabwera akuyembekezera kuti adzapemphereredwe. Nthawi makumi atatu ndi kasanu iye wayendetsa mazana a mailosi, maulendo makumi atatu ndi kasanu.

<sup>12</sup> Ndiyeno kumbukirani, alipo pafupifupi mazana asanu ndi amodzi ndi chinachake akuyembekezera apo...?... mndandanda woyembekezera kuchokera kozungulira dziko kuyesera kuti afike ku kuyankhulana kwapadera. Inu mukuona ...?...zovuta kwambiri. Pamene ife tikungoganiza za pano pokha, iwo sali ochuluka kwambiri. Ife tikhoza kungozimva izo...Mwaona, ndi kuzungulira dziko. Ndipo kotero ife tiri...?...

<sup>13</sup> Ndikudabwa ngati dona ameneyo ali mu nyumba ino usikuuno (ulendo wa makumi atatu ndi kasanu), yemwe analemba kalata kuti adzakhala pano mawa? Kwa nthawi makumi atatu ndi kasanu wakhala ali pano wopanda kukhala atapemphereredwa. Ine ndikuganiza iye sali mu nyumba ino, mwinamwake sanathe kuti abwere konse. Koma ine ndinali kuwerenga chabe kalata yake kumbuyo uko.

Tsopano, ine nthawizonse ndayesera kuti pamene ine ndibwera kuno a...Pamene ine ndiri pa...?...kuti ndiyankhule zokhudza chinachake osati kuti ndizingoyankhula, kapena osati chinachake chomwe chikanati chiwakondweretse anthu...ine ndayesera kuti ndiyankhule za chinachake chomwe chikanati chimukondweretse Mulungu ndi kuwathandiza anthu (inu mukuona?), kwa thandizo, kuti ife tonse tingakhoze, ziribe kanthu kuti ndinu a mpingo wanji, chipembedzo chanji, kuti inu mungakhoze kuthandizidwa kuti muziyenda pafupiko ndi Mulungu. Ndipo ndicho chifukwa chathu cha kukhala pano: kuyenda pafupiko ndi Mulungu.

<sup>14</sup> Ndipo pamene ife tikupeza kuti tsiku momwe liri mochedwa monga ilo lirili, ndi kuyandikira pafupi kwa Ambuye...Ine ndinamuwuza mkazi wanga lero, “Ngati ine sinditi ndilowe mu chitsitsimutso kwinkawake, ine—ine ndifika powonongeka; ine—ine sindingakhoze basi kupirira zimenezo. Ine...Chinachake chiri basi mkati mwanga chikuyaka.”

<sup>15</sup> O! Ife tangobwera kumene kupyola mu mndandanda wonse wa misonkhano kumene zikwi za anthu amabwerako. Ndipo ziribe kanthu ngati iwe ukanakhala ndi anthu mamilioni awiri kapena atatu, ngati palibe chitsitsimutso, ndicho chimene ife tinkachitcha uko mu Kentucky, msonkhano wankhoka. Inu mukudziwa, ife tonse timapita ku msonkhano wankhoka ife tikhoza kuwutcha iwo. Ndipo ife tikufuna chitsitsimutso kumene Mzimu wa Ambuye ukusunthira pa anthu, ndipo anthu akukhala akupulumutsidwa, ndipo zinthu zazikulu zikuchitidwa kuti zikwaniritsire chinachake cha ku Ufumu wa Mulungu.

<sup>16</sup> Ndipo tsopano, mu misonkhano ya mapemphero, kawirikawiri, ife. . . Inu mukhoza kuwona chifukwa chimene ife sitikanakhoza kukhala ndi mzera wa pemphero pano. Mwaona, tangokhala opanikizana kwambiri, iwe sungakhoze kuchita izo. Mwaona? Koma kawirikawiri mu mizere ya pemphero ndi anthu omwe ali—amabwera ndipo iwo amapeza—Ambuye kuti ali weniweni. Ndipo ife tikupeza kuti Ambuye Yesu sanasintho mwakuchepa kumodzi. Kuchokera ku chimene Iye anali, Iye ali lero, ndipo nthawizonse adzakhala ali. Ndipo Baibulo linanena mu Ahebri 13:8, kuti Iye ali Yemweyo dzulo, lero, ndi kwa nthawizonse. Ndipo mu msonkhano wa anthu omwe ankasonkhana kuti amumve Iye mu masiku amenewo, mwinamwake iwo sanali kukhala mu mzera wa pemphero; koma iwo amakhoza kukhala ndi chikhulupiriro kuti akhulupirire. Ndipo Ambuye wathu akanati atembenukireko, pamene chikhulupiriro chawo chikanati chimukhudze Iye, ndipo amakhoza kutembenuka, ndi kuwawuza anthu kuti panali zinthu zinazake zolakwika ndi iwo zomwe iwo anali atazichita, ndi kuti iwo apite ndi kuti achiritsidwe, kapena kupita kukachita chinachake, kukakonza chinachake, kapena chinachake.

<sup>17</sup> Ife tikudziwa za mkazi wa pa chitsime, ndi mkazi wa vuto la magari, ndi, o ochuluka kwambiri, Bartimeyo wakhungu, omwe chikhulupiriro chawo chinamukhudza Iye. Ndipo usikuuno Iye akadali Wansembe Wamkulu wa kuvomereza kwathu ndi basi wamkulu monga Iye anali konse. Tsopano, ife tiyenera kudzilola tokha kukhala antchito Ake. Iye ali Mpesa, gwe—gweru la Moyo. Ife ndife nthambi zomwe zimalandira Moyo umenewo. Ndipo nthambi zimabala chipatso, osati mpesa. Ndipo tsopano, Khristu amagwira ntchito kupyolera mu Mpingo Wake. Ndiyeno, ngati ife tingakhoze kudzipereka tokha mwa njira yotero kuti Mzimu Woyera ukhoza kutenga ulamuliro wathunthu pa ife mu chikhulupiriro chathu mwa Khristu, Iye adzachita chinthu chomwecho, chifukwa ndi Khristu.

<sup>18</sup> Ndipo ngati inu muli pano mlendo ndipo muli nafe. . . Tsopano, kawirikawiri anthu pano. . .? . . . mu kachisi. . . M'busa wathu pano amakhala ndi pemphero la odwala amachita usiku uliwonse. Ndipo inu mumapemphereredwa ndi m'busa wathu wachisomo ndi wokonedwa, M'bale Neville, mwamuna yemwe Mulungu amamumva ndi kumuyankha pemphero lake, M'bale Orman Neville. Ndi—ndi M'bale Don Ruddell, ndi abale ena awo omwe amapempherera odwala. . . Ndi M'bale Jackson, ine ndikuganiza iye ali pozungulira pano penapake kuchokera ku mpingo wina wapaulongo uko mu Howard Park.

<sup>19</sup> Ndipo nthawi iyi pamene ta—tachulukana chomwechi, ngati inu muti mungokhulupirira Mulungu. . .? . . . chirichonse chimene inu muli kuchisowa. . . Ndipo ndinu mlendo ndipo ine sindikukudziwani inu, inu mungomupempha Mulungu ndipo

muwone ngati Iye sali yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse. Muwone ngati Iye sangakhoze kuyankhula pomwe...?...Iye amakudziwani inu; Iye akudziwa chimene chiri chovuta ndi inu; chinthu chokha chimene inu muyenera kuchita...?... mkhulupirireni Iye. Ndiyeno, Iye adzakugwiritsani inu ntchito monga chida chimodzi ndi ine monga chimzake. Yesu anati, Yohane Woyera 14:7, “Iye amene akhulupirira pa INE, ntchito zimene Ine ndizichita iye adzazichita nayenso.” Tsopano, chimenecho ndi chida chodzipereka.

<sup>20</sup> Tsopano, mawa ife tikuti tiphunzitsa momwe iwe umakhalira chida chimenecho, chimene Mulungu, Mzimu Woyera...?...umagwirira ntchito kupyolera mwa iwe. Ndipo chotero...Onani, Iye anali?...Mulungu anali mu lawi la moto, kenako Iye anali—anadzakhala mwa Mwana Wake, Khristu Yesu; tsopano mu Mpingo Wake. Kena Iye ankatchedwa Atate, kenako Mwana, tsopano Mzimu Woyera. Ndi Mulungu kudziwonetsera Iyeyekha kwa dziko. Njira yokha yomwe Iye angakhoze kulowera mu Mpingo inali choyamba kuufera Mpingo kuti awuyeretse Iwo, kuti Iye akakhoze kudziwonetsera Iyeyekha kupyolera mu Mpingo Wake. Ndiye Iye ananena mu Yohane Woyera 15, “Ine ndine Mpesa, inu ndinu nthambi,” (mukuona?) ndipo nthambi imangobala chipatso. Ambuye akudalitseni inu.

<sup>21</sup> Ndipo tsopano, tisanati ife...Kwa phunziro usikuuno... Ndipo ine sindikufuna kuti ndikusungeni inu motalika, chifukwa ine ndikuwawona anthu atayimirira, ndipo wina akutenga malo ake, ndiyeno winayo nkukhala pansu, kupitirira choncho. Ife tikuyesa zolimba kuti tipeze—chilolezo kuti tizikhala pafupi anthu mazana atatu kapena anayi owonjezera, koma a mzinda akuwoneka kuti akutiletse ife pa icho, chifukwa ife tiribe malo okwanira kuyimikapo magalimoto. Ife tinapeza chilolezo kuchokera ku Indianapolis, ndiyeno mzindawu... Ife tiyenera kukhala ndi malo oyimikapo magalimoto. O, pamene ife tingayike anthu anayi mkati muno, ife tiyenera kukhala ndi malo okwanira kuti aziyikapo galimoto kunjwa kuno. Ndipo malo oyikapo magalimoto awa pano kwenikweni ndi a mzinda, kotero, mukuona, iwo... Ndife—tchalitchi chathu kuno changokhala phazi limodzi kuchokera pa mzere wa mzinda. Ndipo—kwenikweni, msewuwawukulu, chifukwa chimene iwo unamangidwira kunjwa uko... Zoono, ena a inu anthu, anyamata aang’ono kuno, simungamvetse izi, koma pano kalelo panali padziwe. Ndipo ine ndikukumbukira pamene ine ndinali mnyamata, ife tinkakwera kubwera pano, ndipo ife tinkachita kupita mozungulira kunjwa uko mmunda ndi kudzafika pa dziwe. Iwo anamanga msewu mozungulira kumene msewu—kuzungulira dziwelo.

<sup>22</sup> Ndipo, ine ndinagula malo awa pano. Tikupemphera pomwe apa pamene ilo liri, Ambuye anandiwuza ine kuti ndigule iwo

pafupi zaka makumi atatu zapitazo kapena zaka makumi atatu ndi ziwiri zapitazo, ndi zimenezo, ine ndikuganiza. Pomwe pano mu dambo lalikulu kwambiri ndi udzu wa kavalo wopitirira pa mutu wanga. . . Ndipo ine ndinagula malowa mtengo wa madola zana ndi makumi asanu ndi limodzi, ngodya ino—pangodya pomwe pano, ndipo ndinamangapo tchalitchi.

<sup>23</sup> Tsopano, Ambuye akudalitseni inu. Ine ndikufuna kuti (ngati iyo ingatchedwe mfundo, zina za. . .), kuwera zina mwa nkhani pa zolemba; ine ndikufuna kuti ndiyankhule kwa omvera usikuuno pa phunziro la *Kukopa kwa Wina*. Ndipo ife tisanayambe kuyankhula kapena kuwera Mawu, tiyeni ife tiweramitse mitu yathu ndi kuyankhula kwa Mlembe wa Mawu.

<sup>24</sup> Ndipo tsopano, ndi mitu yathu yoweramitsidwa ndi mitima yathu. . .? . . . nayonso mu kulemekeza Kwake koyera, ine ndikudabwa ngati alipo ena. . .? . . . usikuuno akanati akhale ndi pempho lomwe iwo—likutentha pa mtima wawo, kuti iwo akanati angokweza. . .? . . . dzanja lanu pamaso pa Mulungu ndi kunena mu pemphero lanu, “Ambuye Yesu, ine ndiri ndi chosowa. Yankhulani kwa ine usikuuno. Ndichizeni ine. Ndipatseni ine zosowa zanga za chuma,” kapena chirichonse chimene icho chiri. Iye amapereka zosowa zathu zonse. Mulungu akudalitseni inu. Pafupi makumi asanu ndi anayi mphambu asanu ndi anayi pa zana a osonkhana.

<sup>25</sup> Atate athu Akumwamba, ife tiri kukuyandikirani Inu. Tsopano pamene ife tikusiya kachisi wamng’ono uyu wa dongo yemwe ife timakhalamo, ngalawa yang’ono iyi yomwe ikupalasa ulendo wakachetechete wa moyo, ndi chikhulupiriro ife tikubwera mmwamba pamwamba pa Marsi, Jupitara, Vinasi, mwezi, nyenyezi, Njira Yamkaka, ndi kufika tsopano mwa chikhulupiriro pa mpandowachifumu wa Atate. Tikumuwona atakhala pamenepo, manja Ake olatsidwa ndi mapazi Ake; mulole Magazi amenewo tsopano apange chitetezero pamene ife tikuyala mphatso zathu pa guwa la golide pozungulira Mpandowachifumu Wake.

<sup>26</sup> Ife tikukuthokozani Inu choyamba chifukwa cha Yesu, Yemwe anapangitsa zinthu zonse izi kutheka kwa ife kupyolera mu chikhulupiriro chathu zomwe ife tikuti tizipemphe. Inu munawona manja, Inu munadziwa chomwe chinali kugunda pansu pa mitima ya anthu. Ndipo ine ndikuyala chikhulupiriro changa Ambuye pa nsembe mu guwa lagolide lalikulu la Mulungu pamene lubano likuwotchedwa tsiku ndi tsiku. Ine ndikupemphera kuti Inu mumve ndi kuyankha mapemphero awo, Atate. Perekani kwa iwo zokhumba za mtima wawo.

<sup>27</sup> Ndipo tsopano, pamene ife tasonkhanira, Ambuye, usikuuno ku kusonkhana kutatu uku, ife tiri muno mu nyumba yotentha iyi usikuuno osati kwa cholinga china koma kuyenda kwapafupiko ndi Inu. Kudziwa choti tichite. . .? . . . Ambuye, choti tichite. . .Monga mneneri ananena, “Iwo

amene ayembekezera pa Ambuye, iwo adzawonjezera mphamvu zawo. Iwo adzakwera mmwamba ndi mapiko ngati mphungu. Iwo adzathamanga ndi kusakhala otopa; iwo adzayenda ndi kusafooka.” Ambuye, tiphunzitseni ife momwe tingamayembekezere titatha kupempha ndipo...?... tikhale nacho chikhulupiriro chodziwa kuti Inu munamva, ndipo mu nthawi Yanu yomwe yabwino Inu mudzatumiza yankho lathu pansa pa makwerero a golide kuchokera ku makonde a Kumwamba kupita mmoyo wathu womwe. Ndipo ife tidzalandira zimene ife tikuzipempha, chifukwa ife tikukhulupirira izo.

<sup>28</sup> Yeretsani makutu athu usikuuno kuti timve ndi mitima yathu kuti tilandire; ndipo mulole pamene msonkhano utha, mulole ife tinene monga awo amene anabwera kuchokera ku Emau, “Kodi mitima yathu siinatenthe mkati mwathu pamene Iye amalankhula kwa ife mu njira yonse.” Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina Lake. Amen.

<sup>29</sup> Ine ndikufuna kuti ndiwerenge usikuuno gawo la Lemba lopezeka mu Bukhu la Yesaya. Mawa, mudzakhale otsimikiza ngati inu muli ndi pepala, ine ndikufuna inu kuti...Ine ndidzakhala ndi chojambulidwa pamwamba pano kapena bolodilakuda kuti ndikhale ngati kujambulapo phunzirolo. Ndipo ine ndikufuna kuti inu muzimvetse zimenezo ngati inu kuli kotheka kuti mungakhoze, chifukwa inu mukhoza kukawerenga izo mukakakhala mutafika kunyumba.

<sup>30</sup> Yesaya mutu wa 6, ine ndikukhumba kuti ndiwerenge ndime pang’ono kuchokera ku mutu uwu kuti ndijambule nkhani—ya usikuuno.

*Mu chaka chimene mfumu Uziya anafa ine ndinawonanso Ambuye atakhala pa mpandowachifumu, wautali ndi wotukulidwa mmwamba, ndipo ulemerero wake unadzaza kachisi.*

*Pamwamba pa iwo panayima aserafi: mmodzi aliyense anali nawo mapiko asanu ndi limodzi; ndi awiri iye anadziphimba nkhope yake, ndipo ndi awiri iye anadziphimba mapazi ake, ndipo ndi awiri iye anali kuvuluka.*

*Ndipo mmodzi anafuulira kwa mzake, ndipo anati, Woyera, woyera, woyera, ali AMBUYE Mulungu wa makamu: dziko lonse liri lodzaza ndi ulemerero wake.*

*Ndipo nsanamira ya kachisi inasuntha pa liwu la iye yemwe anafuula, ndipo nyumbayo inadzaza ndi utsi.*

*Ndiye ine ndinati, Watsoka ndiri ine! pakuti ndine wothedwa; chifukwa ine ndiri munthu wa milomo yosayera, ndipo ine ndimakhala pakati pa anthu a milomo yosayera: pakuti maso anga awona Mfumu, AMBUYE wa makamu.*



*Ndiye anawulukira mmodzi wa aserafi kwa ine, ali nalo khala la moto mu dzanja lake, lomwe iye anali atalitenga ndi mbaniro kuchokera pa guwa:*

*Ndipo iye analiyika ilo pa kamwa yanga, ndipo anati, Taona, ili lakhudza milomo yako; ndipo kusaweruzika kwako kwachotsedwa, ndipo tchimo lako latsukidwa.*

*Pameneponso ine ndinamva liwu la Ambuye, likuti, Ndi ndani yemwe Ine nditi ndimutume, ndipo ndi ndani ati atipitire ife? Ndiye ndinati ine, Ine ndiri pano; nditumeni ine.*

<sup>31</sup> Uku kuli ndithudi—kutengeratu pamene ife tikuganiza za—chomwe chiti chitanthauze pamene ife tiziphunzira masomphenya awa a Yesaya. Ndi...Ine nthawizonse ndamukonda Yesaya. Iye anali mmodzi wa aneneri aakulu. Yesaya analemba Baibulo lathunthu. Alipo Mabukhu makumi asanu ndi amodzi mphambu asanu ndi limodzi mu Baibulo, ndipo Yesaya analemba mitu makumi asanu ndi amodzi mphambu asanu ndi limodzi. Iye akuyamba ndi chiyambi cha chirengedwe; mkati mwa Bukhu iye akubweretsamo Chipangano Chatsopano ndi Yohane Mbatizi; ndipo pa mutu wa 56 ndi 60 iye akutsirizira mu Zakachikwi zopambana: Genesesi kupyola Chipangano Chatsopano mpaka mu Chivumbulutso. Mwamuna wamkulu anali Yesaya uyu. Potsiriza anafa monga wofera pansa pa chilango chachikulu.

<sup>32</sup> Munthu aliyense wodzazidwa-mzimu wa Baibulo anafa kapena anazunzidwa pansa pa boma la feduro. Mmodzi aliyense wa iwo yemwe inu mungakhoze kumuganizira: Mose, ana Achihebri, ndi Daniele, ndi Yesaya. Yesaya anachekedwa mzidutswa ndi machekeka. Ndipo mpaka mmusi, Yohane M'batizi, mmodzi aliyense wa atumwi, Yesu Mwiniwake, onse anafa pansa pa chilango chachikulu kapena chilango chochokera ku boma la feduro. Ndipo malingana ndi momwe zinthu zikuwunjikirana, pakhala pali maumboni ena atawonjezekeredwa kwa awowo limodzi la masiku awa. Mwaona? Ndipo ngati inayamba yakhalapo nthawi yomwe ife tiyenera kumamatirana limodzi, ndi tsopano.

<sup>33</sup> Ine ndikulingalira inu mukumva za msonkhano umene uli kuchitika mu Roma, ndipo ife tiri—iwo ali ndi nthawi yayikulu kumeneko. Ndipo iwo akuti ayambitsa chitsitsimutso. Icho chikhala chitsitsimutso cha dziko lonse, zedi.

<sup>34</sup> Kubwerera ku phunziro ili (ife tidzazipeza zimenezo mu Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri)—ku phunziro ili la kukhala ukukopedwa.

Mfumu Uziya anali mnyamata wolishya. Iye analeredwa... Ndipo iye anakonda kunjira. Ndipo iye analamulira mu nthawi ya uneneri wa Yesaya. Yesaya anali nako kuphunzira kuchokera—kuchokera kwa mmodzi wa aneneri aakulu. Ndipo

ine ndikukhulupirira iye anali Zakariya, kuti Yesaya anali nako kumvetsa kupyolera mwa iye, yemwe anali mneneri pamene Yesaya ankabwera powonekera. Ndipo Yesaya anayitanidwa, ndipo iye anali m—mneneri. Aneneri sali ongopangidwa ndi anthu; aneneri amabadwa ali aneneri.

<sup>35</sup> Tsopano, ilipo mphatso ya ulosi yomwe imabwera mu mpingo, yomwe anthu amapereka ulosi. Ziwalo zambiri za Thupi la Khristu zikhoza kuchita zimenezo, omwe ali pansi pa kudzoza. Koma mneneri amayikidwa mu Mpingo ndi Mulungu, wokonzedweratu ku mphatso ya—ya mneneri—kapena mphatso yoti akhale mneneri, osati wolosera.

<sup>36</sup> Tsopano, tsopano, ife tikupeza kuti mwamuna wamng'ono uyu anatenga mpandowachifumu. Ngati inu mukufuna kulemba ena a Malemba, ndi I Mbiri mutu wa 26. Inu mukhoza kuwerenga pamene amanena kuti Mfumu Uziya atamwalira bambo ake A-m-a-z-i-y-a, Amaziya—iwo atamwalira, pokhala munthu wolungama ndipo anali atatembenuka kuchoka kwa Ambuye, ndipo anaphedwa ndi anthu ake omwe—Uziya anatenga ake—kapena Uziya, kani, anatenga malo ake ngati mfumu. Ndipo iye anakhazikidwa pa mpandowachifumu ndipo anadzozedwa pa usinkhu wa zaka khumi ndi zisanu ndi chimodzi zakubadwa, mnyamata chabe, koma iye anali mu mzere kuti akhale mfumu, komabe pokhala kakhanda chabe. Ndipo iye anachita bwino. Baibulo limatiwuzza ife kuti iye anali nawo bambo aumulungu ndi mayi aumulungu, ndipo iye sakanakhoza kukhala china chirichonse nkomwe ndi kukopa koteroko monga kukhala ali mnyamata waumulungu, chifukwa icho chinakhala chiri chimene chinali chitayikidwa patsogolo pa iye kwa nthawi yonse.

<sup>37</sup> Inu mukudziwa chimene ine ndikuganiza? Aliyense ali nalo lingaliro lake lake. Koma mmodzi wa aakulu kwambiri, ndipo mwa lingaliro langa, purezidenti wamkulu kwambiri yemwe ife tinayamba takhalapo naye mu fuko lino anali Abraham Lincoln. Tsopano, osati chifukwa iye anali wa Republican, koma chifukwa iye anali chimene iye anali, mwamuna waumulungu. Ndipo iye analeredwa, ndipo iye—kuti atumikire Mulungu. Ndipo iye anati, “Ngati pali chirichonse chimene ine ndikufuna kuti ndiperekeko matamando,” iye anati, “kapena moyo wanga unakopedwa naye, anali mayi aumulungu omwe anandiphunzitsa ine kupemphera ndi kuti ndimudziwe Yesu monga Mpulumutsi wanga.”

<sup>38</sup> O! Banja lako ndi chimene iwe uli. Inu mukawalera ana anu mu chikhaliidwe chinachake; iwo ali ndi makumi asanu ndi anayi mphambu zisanu ndi zitanu pa zana mwayi wabwinoko kuti akhale abwino kusiyanana ndi umene iwo ali nawo ngati inu muwalera iwo mu njira yolakwika. “Mulereni mwana mu njira yomwe iye ayenera kuti aziyendamo, ndipo pamene iye akula icho sichidzachoka kwa iye.” Khalani oleredwa bwino,

aphunzitseni ana anu kuti azichita molondola: kuti akhale owona mtima, kuti akhale owongoka ndi achifundo ngakhale pamene iwo ali mu sukulu.

<sup>39</sup> Tsopano, nthawi zambiri ana amakhala ngati akusanzirana kwa wina ndi mzake, ndi—ndi kuyesera kudzikanakizira njira yawo popitirira ndi sukulu. Koma inu mukudziwa, ine ndikuganiza ngati iwe utangoti uzizipeza izo iwewekha, ndiye ndicho chinachake chimene iwe—iwe ukhoza kuyamikira pepala lako lokhoza bwino.

<sup>40</sup> Inu mukudziwa, ngati iwe uti udzakhale ndi mayeso tsiku lotsatira, mmalo momathamanga pozungulira usiku wonse, kudzuka mmawa wotsatira, ndi kuganiza, “Chabwino, ine ndikakhala pafupi ndi *Wakuti-ndi-wakuti*; iwo ndi anzeru; Ndiyeno ine ndikatero—ine ndikhoza kukakopera kuchokera kwa iwo,” ngati iwe ukanangoti Ababa asanabwezere mayamiko pa gome la kadzutsa, ngati iwe ukanangoti, “Ababa, mundikumbukire ine lero, ine ndikuyenera kukatenga mayeso mu khemistre,” kapena chirichonse chimene chiri. Ndiye inu, pamene inu mukupemphera, Ababa, kuti, “Mulungu, mdalitseni Yohane, Maria mu mayeso awo lero.” Ine ndikukuwuzani inu, ilo likatembenuza mafunde.

<sup>41</sup> Kumbukirani, ife tikhoza kukhala nacho chimene ife tikufuna ngati ife tikanati tipemphe mwa chikhulupiriro tikuhulupirira. Yesu anati, “Zinthu zonse ziri zotheka kwa iwo omwe ati adzakhulupirire. Inu simukhala nazo chifukwa inu simumapempha, ndipo inu simumapempha chifukwa inu simumakhulupirira.” Iye anati, “Pemphani mochuluka kuti chisangalalo chanu chikhoze kukhala chodzaza.” Ine ndimakonda zimenezo.

<sup>42</sup> Kuphunzitsa kwathu kolondola: Kunena chinthu cholondola; kuchita chinthu cholondola; kuganiza chinthu cholondola; nthawizonse kukhala ukuganiza molondola. Ndipo ine ndiri nako kuyankhula kwakung’ono:

Chita molondola, ndiyo ntchito yako kwa Mulungu.  
Ganiza molondola, ndiyo ntchito yako kwa iwemwini;  
ndipo ndiwe woti utulukapo wolondola.

<sup>43</sup> Iwe sungati ukhale ukupita kummawa ndi kumadzulo pa nthawi yomweyo, komanso iwe sungati uzikhala ukupita molondola ndi molakwitsa pa nthawi yomweyo. Ziribe kanthu momwe iwe ukuganizira mochuluka kuti ukupita njira inayo, ngati iwe sukuyenda molunjika kumadzulo... Iwe suli kupita kummawa ngati iwe ukupita kumadzulo.

<sup>44</sup> Chotero mfumu yaying’ono iyi pokhala itakopedwa ndi bambo ake pamene iye anali mwamuna wamng’ono ndipo anaphunzitsa Israeli malangizo a Mulungu... Ndiyeno zonse mwakamodzi iye anatembenuka mu masiku ake otsiriza ndipo ankaphunzitsa motsutsa Mulungu. Ndipo anthu ake

omwe . . . Iye anaphedwa ndi anthu ake omwe. Izo zinkawoneka ngati ilo likanakhoza kukhala phunziro lalikulu kwa Uziya pa izi. Koma ife tikupeza kuti pamene Uziya anatenga mpandowachifumu, kuti iye anayamba kumene mu njira yomwe abambo ake anachitira, kubwera nazonso zinthu za Mulungu, kumubweretsa Israeli kubwerera ku kupembedza kwa Mulungu. Iye anadzilimbikitsa iyeyekha.

<sup>45</sup> Ndipo ine ndikufuna nthawizonse kukhala wothokoza kwambiri chifukwa cha iye mu masiku ake awubwana, chifukwa iye sanasewere konse ndale zirizonse. Ngakhale ndale zikanakhoza kukhala zikumutsutsa iye, komabe, iye anakhala molondola pa mzere wa Mulungu. Ndipo icho chinamudolola mneneri wamng’ono, wachichepere uyu, mpaka iye anakhala wopambana. Iye anali chitsanzo kwa Yesaya mneneri.

<sup>46</sup> Ndipo Yesaya anapita ku linga kuti akakhale ndi iye, ku nyumbayachifumu ya mfumu. Iye anamuyitanira iye mkati; iye ankamukonda Yesaya. Yesaya anali wamng’ono nayenso, ndipo—ndipo iye . . . Iwo anali mabwanawe palimodzi. Ndipo momwe mfumu imeneyo . . . Pamene iye amapita kunja uko, ndipo iwo—ena mwa amuna a ndale amakhoza kubwera mkati ndi kuti, “Ife tiyenera kuchita *zakuti-ndi-zakuti*,” Mfumu Uziya choyamba ankafunsira Ambuye. “Ambuye, kodi ndi chifuniro Chanu kuti ife tichite izi *mwakuti-ndi-mwakuti*?” Mulungu tipatseni ife purezidenti wonga ameneyo, osati kokha chimenecho, koma tipatseni ife alaliki. “Funani choyamba ufumu wa Mulungu ndi chilungamo Chake, ndipo zinthu zina zonse zidzachita kuwonjezedwera.”

<sup>47</sup> Ichi chiyenera kuti chinali kukopa kwakukulu, chifukwa Yesaya ankamukonda iye, chifukwa iye anawona kuti iye anali mwamuna wamkulu, ndipo iye—iye anayima njii ndi molimba kwa Mulungu. Ndipo inu mukudziwa, nthawi iliyonse, mu masiku amene ife tikukhalamowa, mu zinthu zimene ife tikuzichita, kumbukirani, anthu sikuti amayang’ana pa m’busa yekha, momwe iye amawonekera—amakhalira, iye—iwo amayang’ana naponso pa anthu wamba.

<sup>48</sup> O, momwe ziriri zoyipa kwambiri pamene ife tiganiza za mpingo. Nthawizina ngati m’busa ali wa chipembedzo *chinachake* kapena mtundu, ndipo bungwe ili likatumizira iye ku mpingo *winawake*, ndipo nthawizina manja a m’busa ameneyo amamangidwa ndi bungwe limenelo. Ndipo munthu wamng’onoyo akufuna kuti awatumikire Ambuye, ndipo iye amaganiza—wakhala ataphunzitsidwa motero za njira yokha yomwe iye angakhoze kuchitira izo, ndi pa kutumikira bungwe lake. Ndipo ngati iye akanayimirira ndi kulalikirira chimene Mawu anena, mpingo ukanakhoza kumuvotera iye achoke; ndiyeno iye amachita mantha iye sakanakhala ndi mwayi ndiye kuti azilalikirira Uthenga.

49 Koma o, chimene ife tikuchisowa mu maguwa lero ndi amuna monga Uziya anali. Ziribe kanthu chimene ndale za mpingo wake kapena ndale za china chirichonse, iye ankasewera mwa dzanja la Mulungu kupyola. Iye ankayembekezera mpaka iye atapeza PAKUTI ATERO AMBUYE, ndiye iye ankachita izo.

Wamng'ono... Mneneri wamng'ono ameneyo (mnyamata wamng'ono wa pafupi usinkhu wake) mkati mwa kachisi ndi iye, iwo anali kugwada pansu limodzi ndi kupemphera, mopanda kukayika, ndi kupempha chifuniro cha Ambuye, ndiyeno nkuchifanizitsa icho ndi malamulo a Baibulo. Ndiye ngati icho chinali chonse cholondola, Uziya ankachidutsitsa icho; ngati icho sichinali cholondola, iye ankatsutsa ndale pa icho. Mulungu tipatseni ife ochuluka onga amenewo! Ndipo chimenecho chinamudolola Yesaya chifukwa iye anabadwa ali mneneri.

50 Ndipo Uziya anakhala—wopambana kwa Yesaya. Inu mukuona iye anali... Chifukwa cha kwake—kuyimira kwake kwa Mulungu, iye anakhala wopambana mu maso a wolungama. Ndipo uko mwina kukhoza kuti kunalibe olungama ochuluka kwambiri. Mwaona? Koma chinthu chimene ife tikufuna kuti tichite, ndi kupanga moyo wathu kuwerengedwera kwa Mulungu. Winawake akukuyang'anani inu.

51 Ine ndinali kumunena winawake tsiku lina. Mwa oyandikana nawo ena iwo anali ndi... Mpingo wawukulu wa chipembedzo anali ndi phwando lalikulu la kwasakwasa kumusi kuno, ndipo iwo anali akuvina mpaka pafupi 1 koloko mmawa. Ndipo iwo anali akumunena winawake yemwe amabwera ku kachisi, ndipo anati iwo anali oyera odzigudubuza omwe anabwera kumusi kuno, chifukwa ife tiribe chipembedzo. Ndipo o, momwe izo zinandipatsira ine mwayi. Inu mukhoza kungolingalira kokha chimene chinachitika. Koma chinthu cha icho chiri... Tsopano, anthu amenewo... Mopanda kukaika, dona wamng'ono ameneyo amene anapanga ndemangayo, ngati iye akanadziwa kokha chimene chinali Choonadi... .

52 Ine ndinali mu mapiri masabata angapo apitawo. Ndipo kutali komwe pamene ine ndinali kubwera kunyumba, ife tinabwerera (banja ndi ine) kuti tikapumule pang'ono, kumene ife tikupita kachiwiri, Ambuye akalola, sabata lamawa. Ndiyeno, kumbuyo uko usiku umodzi, ine ndinawona masomphenya. Ndipo iwo anali w—wokondeka, mkazi wokongola, ankawoneka mkazi wamng'ono akuthamanga; iye anali ndi dzanja lake apo, ndipo iye anali akufa ndi vuto la mtima, mkazi wokongola. Ndipo iye anagwa ndipo anali atapita. Ndipo Mngelo wa Ambuye anati, "Tsopano, pamene iwe uti umve ichi, kumbukira, iwo azikanena kuti iye anachita kudzipha, koma iye anafa mu vuto la mtima. Ndipo iyo ili pafupifupi 4:00 koloko, kotero iwe ukangoti 4 koloko," ndiyeno iye anandichokera ine.

<sup>53</sup> Ndipo ine sindinalidzutse banjalo mu hema wamng'ono wa ng'ombe (kapena kumene anyamata osalishya ng'ombe amakhalako, kumene ife tinkapitako pobwerera uko kuti tikakuse ng'ombe), ine—ine ndinangowasiya iwo agone mpaka mmawa. Ndiyeno, tsiku lotsatira ine ndinanena izo, ndipo ine ndinati, “Mkazi wina wamng'ono, wokongola kwambiri, ndi woti afa—mwa vuto la mtima.” Ndipo pa msewu tikutuluka masiku awiri kenako, apo izo zinabwera umo pa wailesi kuti Abiti uyu (ine sindingakhoze kulingalira za dzina lake) Monroe, Akazi a Monroe. Ine ndikuganiza limenelo linali dzina lake la pasewero, kapena chirichonse chimene ilo linali; dzina lake lina la chinachake. Ndipo iye anali atafa, ndipo iwo anati iye anachita kudzipha.

<sup>54</sup> Tsopano, izo sizikupanga kusiyana kulikonse kaya ine ndinena mochuluka bwanji izo; iwo azinenabe kuti iye anachita kudzipha. Koma mwanayo sanatero ayi; iye anafa mu vuto la mtima! Ndipo ngati inu mukanati muyang'ane, iye anali ndi dzanja lake, akuyesera kuti afikire ku foni—foni ili mu dzanja lake. Iye anali ndi vuto la mtima. Iwo anati mapilisi atulo anali pamenepo; iye anali akuwamwa iwo kwa mwezi (mwaona?) kapena kuposa, kuchokera mu botolo limenelo. Iye anafa mu vuto la mtima, ndipo iye anafa pafupi mphindi folo kapena faifi isanakwane 4 koloko, kwenikweni.

<sup>55</sup> Ndipo ine ndinawerenga za mbiri ya moyo wake mu magazini momwe kuti iye . . . Iye anali mwana wamchigololo; ndi momwe kuti iye anali atatsuka mbale zambiri; ndipo mayi ake ali ku malo a amisala; ndipo iye ankakhumba (koma iye anali mkazi wa thupi langwiro kwambiri, ine ndikuganiza, mu dziko)—koma iye ankakhumbira chinachake chimene ndalama sizikanakhoza kugula. Ine ndinaganiza, “O, ine ndikukhumba ine ndikanafika kwa iye! Ine ndikudziwa chimene iye ankachisowa!” Apo inu muli!

<sup>56</sup> Mwina wake mamembala a mipingo yotchuka, yabwino kwambiri—Hollywood yotchuka, kumene kukongoletsa konse ndi zowala ziriko . . . Koma iwo ankawawona anthu amenewo . . . Iye amakhoza kuwawona kuti iwo samakhala moyo wosiyana kuposa umene iye ankakhala. Izo zimatengera kukopa! Izo zimatengera mphamvu ya chiwukitsiro cha Khristu pakati pa anthu, kuti awone kuti Khristu sali choyimikidwa chitapachikika mu nyumba, koma Iye ndi Chinthu chamoyo mu mawonekedwe a Mzimu Woyera, akukhala mwa amuna ndi akazi, akubweretsa mtendere, ndi kukondweretsedwa, ndi chisangalalo. O, ngati ife tikanakhoza kokha kufika kwa dona wamng'onoyo iye asanalisiye dziko.

<sup>57</sup> Tsopano, kukopa. Ife tikupeza kuti—kuti moyo wa Uziya unamukopa mneneri uyu mpaka pa malo otero kuti Ukiya—Uziya, kani, anamanga makoma ndi kudzilimbikitsa iyeyekha, ndipo anatenganso malo ndi zinthu zomwe zinali za iwo

kuchokera kwa Afilisti, ndi zina zotero, mpaka kutchuka kwake kunapita njira yonse kukafika ku Igupto. Ndipo ine ndikukuwuzani inu, mwa mbiri zonse za mafumu, panalibe mmodzi mwa iwo kunja kwa Solomoni, yemwe anafalikira chotero monga Uziya. Chifukwa chiyani? Chifukwa iye anayika chitsanzo. Iye anakhala ndi Mulungu, ziribe kanthu chimene anthu ake ankaganiza, chimene wina aliyense ankaganiza, chomwe andale ake omwe ankayesera kuti amukope iye. Iye anakhala molunjika ndi Mulungu, ndipo icho—Mulungu anamudalitsa iye. Ilo linali thandizo lalikulu kwa mneneri wamng'ono uyu.

<sup>58</sup> Momwe Mulungu amamudalitsira munthu yemwe ati akhale woona ku Mawu a Mulungu. Tsopano, iye mwina sati akhale wotchuka kwambiri, koma iye akhala ali wodalitsidwa. Ndipo tsopano, anthu ayenera kutenga kusankha kwawo, kaya inu mukufuna kuti muzichita monga anthu enawo kapena inu mukufuna kuti mukhale odalitsidwa ndi Mulungu. Tsopano, inu mukhoza kungotenga kusankha kwanu. Ngati inu muti muzikhala monga ena onsewo, inu muzikhala odalitsidwa ndi iwo; koma inu mukatembenezira zanu—zokhumba zanu zonse kwa Mulungu, ndipo inu muzikhala odalitsidwa ndi Mulungu. Kotero inu muyenera kutero “Sankhani inu tsiku lino yemwe muti muzimutumikira,” monga mneneri ananena. “Nthawizonse kumbukira Mlengi wako, choyamba, nthawizonse.”

<sup>59</sup> Tsopano, koma . . . Pamene mfumu iyi inafika pa malo, pokhala munthu wamkulu chotero ndi kumamukopa Yesaya ndi wolungama, ndithudi, a ufumu wake, iye anafika pa malo—iye anayamba kumverera kutetezeka kwayekha. Ndipo pamene ndi pomwe inu mumapangira kulakwitsa kwanu. Pamene ndi pomwe anthu ochulukira kwambiri olungama amaluma fumbi la manyazi, amaluma fumbi la kugonjetsedwa, ndi chifukwa chakuti iwo amayamba kumverera otetezeka mwaokha. Iwe umayamba kuganiza kuti iwe wakhalira Khristu moyo motalika chotero, kuti palibe kanthu chimene Iye angapereke kwa iwe, iwe utenga kusankha kwako ngati ukuchifuna icho kapena ayi. Iwe uyenera kumapitiriza kumutumikira Mulungu. Ziribe kanthu chomwe iwe unali mmbuyo zaka khumi zapitazo, ndi chimene iwe uli tsopano.

<sup>60</sup> Mfumu inafika pa malo amene iyo inkaganiza mkati mwa iyemwini, kuti iye anali atakwezeka pamwamba. Kunyada kunafika mu mtima wake. Ndipo ndi chimene chimachitika kwa ife. Ngati inu mungakhululukire kuyankhula uku, ndicho chimene chachitika kwa mipingo yathu konsekonse mu dzikoli. Iwo ndi anthu abwino mkati mmenemo; ena a abwino kwambiri mu dziko amapita ku mpingo. Ine ndikuganiza abwino kwambiri mu dziko amapita ku tchalitchi. Koma chinthu cha icho chiri, k—kachitidwe ka bungwe kamakhala katakwezeka pamwamba. Ndicho chimene chinachitika kwa—Amethodisti;

ndicho chimene chinachitika kwa Abaptisti; ndicho chimene chinachitika kwa Anazereni, kwa a Pilgrim Holiness, kwa Apentekoste—anakwezeka pamwamba, odzifunira okha, ochita zaokha, onyada, mwakuti iwe sungati uwawuze kanthu. Mulungu sangakhoze kupeza njira yoti alowere mu mitima yawo. Ndi chifukwa iwo amakhala odziwa-izo-zonse mwakuti palibe munthu wina angakhoze kuwawuza iwo chirichonse. Ndipo pa kudzimangira okha mozungulira kulingalira ndi abale, iwo amadzimangira okha mozungulira chikhulupiriro chawo. Ndipo pamene iwo atero, iwo amamusiya Mulungu mmbuyo.

<sup>61</sup> Ndicho chimene chimachitika kwa madokotala. Pamene iwo afika pochita-zawokha mwakuti iwo sasowa thandizo lililonse lochokera kwa Mulungu, ndi pamene ine sinditi mmodzi—sindifuna mmodzi azipusitsana ndi ine. Pamene iwe umusiya Mulungu kunja kwa chirichonse, iwe basi—ine ndikufuna iwe undisiye ine kunja nanenso. Mwaona? Chifukwa iwe uyenera nthawizonse kukumbukira Mulungu choyamba! Iye anali atakwezeka pamwamba.

<sup>62</sup> Chotero ambiri lero... Inu mutenge—banja la anthu lomwe liti liyambe kupita ku tchalitchi. Ndipo Mulungu alichiza banja laling'ono limenelo. Iye awadalitsa iwo, ndi kuwapatsa iwo Mzimu Woyera mu miyoyo yawo. Ana aang'ono ali kupemphera pozungulira gome; iwo kukhala akumapemphera asanapite kokagona. Mayi ndi bambo kulumikizana manja ndi kumapemphera. Ndipo malingana ngati iwo azipitiriza monga chomwecho, iwo adzakhala monga banja; koma inu muwalole iwo apeze... Chinthu choyamba inu mukudziwa, iwo analibe kalikonse, chiphakasa cha galimoto chakale, mwinamwake, akukwera pozungulira mu icho, kapena mwinamwake akuyenda. Potsiriza iwo apeza galimoto yabwino, nyumba yabwinoko. Ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, ndiye iwo amafuna kuti afike ku chimene iwo—dziko limachitcha, kalasi yabwinoko kuti aziyanjana nalo. Iwo amasunthira ku malo osiyana, ndipo mkati mmenemo, iwo amapeza kuti iwo amakhala okopedwa ndi kukopa kolakwika. Inu muyenera nthawizonse kumakhala kumene Ufumu wa Mulungu uli ndi kumene ulemerero wa Mulungu ukutsanulidwirako. Khalani kumene inu mungakhoze kukhala mukudyetsedwa mwauzimu usana ndi usiku. Ndiye chinthu choyamba inu mukudziwa, kusiyana kumabwera mu nyumba, ndi chidziko, ndipo iwo amakhala atakwezeka pamwamba. Uziya anachita zimenezo; iye anali atakwezeka pamwamba, kunyada kochuluka.

<sup>63</sup> Ndipo tsopano, ife tikuwona chimene iye anayesa kuchita. Tsopano, chimene kwenikweni chinamugwira iye pamene iye anali atakwezeka pamwamba mu mtima mwake (ife tikuwuzidwa mu Baibulo, mu Mbiri ya 26—ife tikupeza—ll Mbiri 26), ife tikupeza kuti iye anapita kukalowa mu kachisi wa Ambuye ali ndi chofukuzira mu dzanja lake kuti akawotche



lubano kwa Ambuye. Ndipo pamene iye anatero, mtumiki wa kachisiyo ndi atumiki ena makumi asanu ndi atatu anamutsatira iye ndipo anamuwuza iye, “Musati muchite zimenezo; inu mukulakwitsa. Inu sindinu mtumiki. Inu ndinu mfumu, osati mtumiki.”

<sup>64</sup> Ndipo iye anali wokwiya, ndipo iye ananyanyuka. Ndipo mkwiyo wake unafika patali ndi iye, ndipo iye anayatsa zofukizirazo kuti apite mulimonse. Ndipo Mulungu anankantha khate pa iye apo pomwe pamene iye anali atayima pamenepo mu kukwiya kwake; ndipo iye anafa wakhate. Iwo anachita kumutengera iye kunja kwa kachisi.

<sup>65</sup> Apo ndi pamene ife tikufuna phunziro tsopano. Ngati munthu uyu yemwe Mulungu anali atamudalitsa mwa muyezo wake...Koma iye sanali wokhutitsidwa ndi zimenezo, iye ankafuna kuti atenge malo a munthu winawake. Iwe sungakhoze kukhala kanthu...Monga munthu wa Kongeresi Upshaw (inu mukumukumbukira iye, mmodzi yemwe anali—anali wolumala kwa zaka makumi asanu ndi amodzi mphambu zisanu ndi zitatu ndipo anachiritsidwa mu msonkhano kunja uko, inu mukudziwa. Iye anali munthu wa Kongeresi wa ku United States.), iye anati, “Iwe sungakhoze kukhala kanthu kamene iwe siuli.” Koteri ndizo pafupi zoon. Iwe uyenera kuti ukhale mu kuyitana kwako, kumene Mulungu anakuyitanirako iwe.

<sup>66</sup> Tsopano, motalika momwe iye anangokhala ali mfumu, ndipo—iye anali mdalitso kwa anthu pokhala mfumu. Koma pamene iye anaganiza kuti iye anali mtumiki, ndiye...Iye anaganiza chifukwa Mulungu anali atamudalitsa iye, iye akanakhoza kukhala chirichonse chimene iye ankafuna kuti akhale. Koma iye anali mdalitso kwa anthu monga mfumu, koma osati mdalitso...Iye anakhala themberero pa iwo pamene iye anayesera kuti atenge malo a mtumiki. Ndipo ife tiri ndi zochulukira za zimenezo. Aliyense akufuna kuti awutenge mpira. Mukuona?

<sup>67</sup> Pamene inu mukusewera masewero a mpira (pamene iyo ili nyengo ya mpira wa miyendo), chinthu chimene ife timafuna kuti tichite, sichiri aliyense kuyesera kuti awutenge mpirawo kuchokera kwa munthu yemwe ali nawo iwo; ndi kuyesera kuti umutetezere munthu ameneyo. Kumuteteza iye; kumulola iye kuti adutse nawo. Ife tikuyesera kuti tipange chigoli. Mwaona?

<sup>68</sup> Koma inu mungakhoze kulingalira mfumu yosaphunzitsidwa chotero kuti itapeza munthu mmodzi—munthu wawo yemwe—ali ndi mpira akuthamangira kogoletsera kwa bwalo, ndiyeno mmalo moyesa kuti umugunde mdani achoke kwa iye, gulu lomenyana nalolo, kuti amulole munthu wawo yemwe ali nawo mpirawo athamange nawo iwo, munthu aliyense akuyesera kuti awutenge mpirawo kuchokera mu dzanja lake? Bwanji, inu ndinu oti mugonjetsedwa.

<sup>69</sup> Ndipo lero, ife tiri ndi chinthu chomwecho. Pamene ife tiwona Mulungu akubwera powonekera, ndipo akuti adalitse chinthu chinachake, tiyeni tiyingitse adani onse atalikire kwa icho. Tiyeni tigwiritse ntchito kukopa kwathu monga otchinga, osati othamanga, otchinga omwe amamuteteza wothamanga, timulole iye awutenge mpirawo nkudutsa nawo, chifukwa palibe wotsutsa, chonse chimene inu muyenera kuchita ndi kupitirira kuthamanga. Ndipo ife tiyenera kukhala otchinga.

<sup>70</sup> Ine ndimayankhulira mu dziko monse, inu mukudziwa, Amuna Amalonda a Uthenga Wonse, kuzungulira dziko, kukonza machaputala. Ndipo osati kale litali pamene, ine ndikukhulupirira, iko kunali ku Kingston, Jamaica, pamene iwo anali ndi Castro ndi onse a iwo kuntunda uko pa msonkhano umenewu (kapena ife tinali tiri kumeneko ku malo ake, ndimo momwe izo zinaliri), ndipo olemekeseka a konse ku zilumba zonse anali kumeneko; ndipo amuna amalonda amenewo anali kuyesera kulalikira Uthenga. Iye wachoka pa malo ake. Ife alaliki timakhala ndi nthawi yovuta mokwanira kuti tiziyike izo pa muyezo. Ndipo iwo amagwiritsa ntchito kukopa kwakung'ono kumene iwo angakhoze kukupeza, ndi kandale kakang'ono kalikonse njira *iyi* ndi njira *iyoyi*, ndi kuziika izo posokonezeka kwambiri mwakuti iwe sudziwa choti uchite.

<sup>71</sup> Nthawi zambiri ku—mu mpingo—mpingo waung'ono ukhoza kukhala ndi chitsitsimutso chiri kuchitika; winawake angafune kupita kunja kuno ndi kukatsogolera msonkhano wa mapemphero. Ndiyeno, iye amakhala ndi lingaliro losiyana kuchokera ku chimene kwenikweni Baibulo limanena, koma iye akukhulupirira izo mwa njira *iyi* mulimonse; ndipo iye amayamba kukopa ndi kuwakokera ena kuchokera ku ilo. Chinthu choti uchite chiri kuuteteza Uthenga uwu momwe Iwo ukuyendera, khala limodzi nawo Iwo, ndipo gwetsera chirichonse kutali kuchokera kwa Iwo, ngati ife titi tikawoloke konse mzere wa magolo.

<sup>72</sup> Ndipo ine ndinati, “Abale, pali chinachake cholakwika. Inu anyamata ndinu amuna amalonda. Malo oyamba, inu simumamvetsa mafikidwe. Inu simumamvetsa mafikidwe a ku utumiki, chifukwa utumiki ndi mphatso yoitanidwa ndi Mulungu.” “Mulungu wayika mu Mpingo choyamba atomwi, aneneri, aphunzitsi, alaliki, ndi abusa.” Mulungu anawayika iwo mmenemo pochititsa ungwiro Mpingo. Amuna amalonda ayenera kumachitira umboni. Akazi, mkaziwamnyumba, ziribe kanthu ngati muli wantchito mu nyumba ya winawake, zichitirani umboni. Chitani chirichonse chimene inu mungakhoze chifukwa cha Ufumu; koma musati konse muzibayiramo malingaliro anu anu; zingonenani chimene Uthenga ukunena ndipo khalani mukupitirira patsogolo (mwaona?), ndiyeno mwinamwake inu mungakhale nako kukopa kwina. Chabwino, musati muyesere kuti muzilalikira

tsopano mpaka Mulungu, inu mudziwa, akakuyitanani inu. Ingokhalani kumene ndi chimenecho, umboni wanu, chifukwa ngati inu simutero, inu mukalowa mu gulu lolakwika; ndiyeno inu mudzasokoneza chirichonse. Ndi zimenezotu. Ndipo izo sizimamukondweretsa Mulungu nkomwe. Izi zikutsimikizira izo pano.

<sup>73</sup> Pamene mfumu iyi . . . Tsopano, pamene iye anadzudzulidwa ndi kuwuzidwa zooni ndi mtumiki wa nyumbayo, ndi kuyesa kuti amuwuze iye kuti iye anali kulakwitsa, kuti Mulungu anayitanira izo obadwa kuchokera kwa Aaroni okha, ndipo iwo anali opatulidwira ku utumiki umenewo wokha . . . Ndicho chonse chimene iwo anali oti azichita, iwo anali opatulidwira ku chimenecho. Ndipo mfumu, ziribe kanthu momwe iye anali wolungama, kapena mochuluka chotani Mulungu anali atamudalitsa iye, iye anali wopanda ufulu kuti awotche lubano. Iye anali akutenga malo a wansembe, ndipo iye sayenera kuti azichita zimenezo. Ndipo pamene iye anadzudzulidwa, iye anakhala wokwiya; mkwiyo wake unakwera mmwamba, ndipo pamene kukwiya kwake kunakwera mmwamba, khatelawonekera mu nkhope yake. Iye anakhathamira ndi khate, ndiyeno iye anagwetsa chofukizira ndipo anathamanga kutuluka mnyumbamo. Mwaona? Kuyesera kuti amusanzi munthu winawake, ife tisati tizichita zimenezo.

<sup>74</sup> Mu kukwiya kwake iye anachita cholakwika, ndipo iye anakanthidwa. O, ilo linali ndithudi phunziro kwa mneneri wamng'ono uyu kuti awone, tsopano, ziribe kanthu momwe munthuyo analiri wamkulu, iye ankayenera kuti azikhalabe mu kuyitanidwa kwake.

<sup>75</sup> Ine ndikuzindikira kuti izi zikujambulidwa, ndipo ine ndikudziwa kuti izo zitero—zimapita konse mu dziko, uko ku nkhalango, ndi Akafula, ndi chinthu chirichonse. Uthenga uyu pano usikuuno ukakhala utamasuliridwa mu zinenero. Koma ine ndikunena ichi ndi mtima wanga wonse, zingakhoze bwanji . . . Anthu ambiri akuti, “Bwanji inu simukujowina mabungwe enaake? Nchifukwa chiyani inu simukubwera uko ndi Achipentekoste? Nchifukwa chiyani inu simukungolola zinthu zazing'ono izi zizipita?” Ine ndingakhoze bwanji kuchita izo? Ine ndiyenera kukhala ndi Uthenga umenewo!

<sup>76</sup> Pamene Mngelo wa Ambuye anawonekera uko pa mtsinje mu Kuwala kuja kumeneko monga inu mukukuwona, ndipo pamene izo zatsimikiziridwa ndi boma ndi kwina kulikonse, ndi sayansi—kafukufuku wa sayansi kuti ndi zooni . . . Ndipo Iye anandiwuza ine kuti ndikhale ndi Mawu awa. Ndiye ine ndingakhoze bwanji kusinthanitsa Iwo ndi kachikhulupiriro? Ngati amuna amenewo ali kunja uko akuti azichita zimenezo, asiye iwo azichita izo. Koma ife tinayitanidwa kuti tizilalikira Mawu! Musati munyengerere; imani pa Mawu!

<sup>77</sup> Kotero tsopano inu mukuwona chifukwa chomwe chiri chinthu chowopsya kuti uyese kunyengerera ndi kumachita chinthu chinachake, kapena kuyesa kukhala wokwezeka pamwamba mwa iwemwini, ndi kunena, “O, ine ndingakhoze kuchita *izi* ndi kupanga ndalama zochulukirapo. Ine ndikhoza kuchita *izi*, ndipo abale onse adzagwirizana nane.” Ine ndikhoza kunyengerera pa Mawu awa, ndi—mpaka makumi asanu ndi anayi mphambu asanu ndi anayi pa zana a atumiki adzatembenukira kumeneko, “Izo ndi zabwino, izo ziri bwino.” Ndipo ine ndikudziwa tsopano, ambiri a iwo amazitcha... Ndi chiyani icho? Mikate ndi nsomba, kuwawona anthu akuchizidwa, ndi kuzindikira za mmitima, ndi mphamvu za Mulungu, ndi zina zotero, zikuwonetseredwa. Iwo amakutengera iwe kumeneko kuti ukatenge misonkhano ndi kuti uwatengere anthu mu—mipingo yawo ndi zinthu; koma pamene izo zifika pa kugwirizana pa Mawu, iwo amachoka kwa Iwo. Mwaona? Iwe sungakhoze kuchita zimenezo. Khala ndi Mawu!

<sup>78</sup> Tsopano, ili linali phunziro kwa mneneri wamng’ono uyu, kuti palibe kanthu chimene iye ankayesera kuti akhale, iye ayenera kukhala mu kuyitanidwa kwake. O mai, iye anaphunzira do—dongosolo la Mulungu kwa munthu. Dongosolo la Mulungu kwa munthu ndilo kukhala mu malo ake. Dongosolo la Mulungu kwa akazi ndilo kukhala mu malo awo nawonso. Inu simungakhoze kutenga malo a mwamuna. Iwo akuyesera kuti azichita zimenezo, koma musati muchite zimenezo. Mwamuna, asati atenge malo a akazi, asati azivala monga akazi. Ndipo akazi musati muzivala monga amuna. Baibulo limati ndi cholakwika kuti uzichita zimenezo. Baibulo limati, “Mkazi yemwe amavala chovala cha kwa mwamuna, ndi nyansi pamaso pa Mulungu, ndi themberero.” Mwaona? Koma tsopano iwe sungathe kusiyantsa nkomwe wina kwa mzake. Mwaona? Tsopano, iwe uti uzichita motani, koma kungozitchula motsutsa izo? Chabwino, ndiye pamene iwe uchita izo. . .

<sup>79</sup> Kodi inu munawona lamulo la bwalo la milandu ili sabata lino mu Indiana? Nchamanyazi bwanji! Kuchepera zaka khumi ndi zisanu zapitazo banja kuno mu Port Fulton (ine ndikuganiza ena a banjala ali muno usikuuno)—kuno ku Port Fulton, iwo anamutumiza msungwana wamng’ono kwawo kuchokera ku sukulu chifukwa chovala kabudula ku sukulu. Ndipo ku—sabata lino iwo akuyesera kumusumira ndi kumuchotsa ku sukulu (ndipo iwo achita zimenezo), msungwana wamng’ono yemwe akukana kuvala kabudula mu sukulu. Chavuta ndi chiyani ndi fuko lathu? Ine ndimaganza ili linali dziko la ufulu; ine ndimaganza ife tinali ndi ufulu—ufulu wachipembedzo.

<sup>80</sup> Bambo uyu anayimirira ndipo anati, “Ndi chotsutsana ndi chikhulupiroro chatu chachipembedzo kuti ana athu azivala kabudula, msungwana wathu wamng’ono wa khumi ndi zisanu ndi chimodzi, wa usinkhu wa zaka khumi ndi zisanu ndi ziwiri,

kuti azivala makabudula; ndi chotsutsana ndi chikhulupiriro chatu chachipembedzo.” Ndipo iwo sanazisamale ndipo anamuchotsa mwanayo ku sukulu.

<sup>81</sup> Ine ndamva kuti aliyense yemwe sati avomereze ndi kubwera mu—mu—mgwirizano wa dziko lonse wa chiyanjano ichi umene iwo akuyesera kuti awuyambitse kuti awuyike—ndi kulumikiza mipingo yonse palimodzi, chitaganya cha mipingo, kuti onse amene sati abwere mmenemo ndi kuyanjana nacho icho, iwo akuwakonzera iwo ka malo kakang’ono; iwo akuti awatumize iwo ku Alaska. Inu mwina muzikonzekereratu nyatungo yozizira, chifukwa izo zikuwoneka ngati zikubwera. Kotero, ndi chamanyazi bwanji!

<sup>82</sup> Bwenzi langa la utali wa moyo, Jim Poole, mwana wake wayima pano usikuuno. Ine ndimakhumba abambo ake akanati angobwera ndi kudzaona chimene mwana wao wachita. Ndipo ife tinali kuyankhula lero pa kuyankhulana kwa pa telefoni, ndipo iye anali kuchitira ndemanga zokhudza, ine ndikukhulupirira, wochitira ndemanga kapena winawake, (ine sindikukumbukira basi ndani yemwe uyo anali tsopano), koma anati, “Izo zinkakhala kuti—kuti anthu Achimereka anali kusamba kamodzi pa sabata ndi kupemphera tsiku lirilonse,” ndipo anati; “tsopano iwo amasamba tsiku lirilonse ndi kupemphera kamodzi pa sabata.” Ine ndikukhulupira ine zikanakhala bwino ndikhale wopanda kusamba. Koma zikungosonyeza momwe ife tagwera. Chachitika nchiani kwa fuko ili?

<sup>83</sup> Pafupi zaka zisanu zapitazo ine ndinali mu Ohio, ndipo ine ndinali ndikuchititsa msonkhano kumtunda uko ku (ndi chiyani dzina la malo amene aja kumene ine ndinali nawo iwo kunja uko pa chijachi? [Winawake akuti, “Chataqua”—Mkonzi.]—Chataqua. Ndipo ine ndinali kumvetsera ku kuwonetsa kwa nkhani mu hotelo, ndipo iyo inati, “Duwa la ufulu lafa madzulo ano mu bwalo la milandu kuno mu Ohio.”

Anthu Achiamishi, iwo samakhulupirira mu kutumiza ana awo ku sukulu izi za aliyense. Iwo ali nawo masukulu awo awo. Ndipo mwa oyandikana nawo enaake awa kumene izi zinali, iwo analibe masukulu apamwamba aliwone. Ndi lamulo la Ohio ndi Indiana (ine ndikuganiza lamulo la fuko) kuti ana onse ayenera kumapita ku sukulu mpaka iwo atafika khumi ndi zisanu ndi chimodzi. Ndipo bambo uyu anali ndi ana awiri, mnyamata ndi msungwana, omwe sanali khumi ndi zisanu ndi chimodzi; ndipo iwo amakana kuti awatumize iwo ku masukulu a aliyense kumene iwo amaphunzitsa maganizo a Darwin (kuti munthu anapezeka kuchokera ku selo imodzi, nkukhala nyani; ndicho chonse chimene iye ali, ndi nyani waulemerero basi ndi. . .). Ndipo chotero, iwo sanali kugwirizana nazo zimenezo, ndipo iwo sanali kuwalola ana awo kuti azimva zimenezo. Ndipo kotero mabwalo amilandu anawakokera iwo mkati. Ndipo woweruza

wodziona ngati wanzeru wamng'ono uyu ananena kwa bambo wamkulu wachikalambire ndi mayi, ali ndi tsitsi lake lodula pamphumi ndipo atavala maovololo, iye anati, “Bwana, boma ili la Ohio liri ndi lamulo limene limanena kuti ana ayenera kumapita ku sukulu kufikira ali wakhumi ndi zisanu ndi chimodzi,” ndipo anati; “inu mukukana kuti muwatumize ana anu. Kodi inu muyankha chiyani?”

<sup>84</sup> Iye anati, “Wolemekezeka bwana, ine ndikulemekeza malamulo a boma lokondeka ili mmene ine ndiri mbadwa.” Iye anati, “Koma ife tinabwera kuno zaka zapitazo, makolo athu akalewo, chifukwa cha ufulu wa chipembedzo, ndipo ndicho chifukwa ife tiri kuno, chifukwa cha ufulu wa chipembedzo. Chipembedzo chathu chimatiphunzitsa ife kuti ife sitimakhulupirira kuti ife timabwera kuchokera ku zinyama kuti tikhale munthu kuti . . . Ife timakhulupirira kuti ife tinalengedwa mu chifaniziro cha Mulungu. Chotero, ndi chotsutsa zikhulupiriro za chipembedzo zathu kuti tiziwatumiza ana athu ku sukulu zomwe zimaphunzitsa zoterozo. Chotero, ife tiribe sukulu yapamwamba iliyonse kuno kuti ana athu azipitako. Ndipo si chifukwa chakuti ife sitimakulemekezani inu; ife timalemekeza chimene inu mumakhulupirira; koma kwa ife, ife sitimakhulupirira zimenezoz, ndipo ife sitikufuna kuti izo ziziphunzitsidwa kwa ana athu.”

Iye anati, “Inu mwina muwatumiza ana anu ku sukulu kapena inu ndi akazi anu mukatha zaka ziwiri mu ndende ya boma.” Anati, “Lingaliro lanu ndi lotani?”

Iye anati, “Mayi ndi ine tikatha zaka ziwiri.” Ndipo iwo anatembenuka ndi kuyamba kupita panja.

Woweruza wakaleyo ayenera kuti anamverera kutsutsika pang'ono, kotero iye anati, “Kumbukirani, kodi Baibulo lanu silimati, Mpatseni Kaisara zomwe ziri za Kaisara?”

Ndipo bamboyo anatembenuka mozungulira, ndipo iye anati, “Ndipo kwa Mulungu?”

Mwamuna wa pa nyuzi anati, “Chabwino, ndiye ufulu . . .”

Ndipo woweruzayo anati, “Ine ndikukuweruzani inu ku zaka ziwiri.”

Iye anati, “Ndiye ufulu—duwa la ufulu lafa mu chipinda chamilandu icho madzulo ano.”

<sup>85</sup> Kuwonjezera apo, Achidunkardi—kapena Achiamishi, kani, ziribe kanthu momwe iwo aliri achilendo, iwo amakhulupirira mu kukhala moyo woyera. Ndipo palibe umboni umodzi uliwonse mu United States kumene iwo anayamba akhalako ndi kupanda makhalidwe kwa ana. Palibe munthu mmodzi, mwana mmodzi, kuchokera ku chipembedzo chawo anayamba wakhalapo ndi kupanda khalidwe kwa ana. Asiyeni iwo akhale achilendo chirichonse chimene iwo akufuna kukhala; iwo amaleredwa bwino. Ine sindikuwatsutsa iwo.

<sup>86</sup> Koma mvetserani, duwa linafa pamenepo nthawi yomweyo, koma pafupi maminiti khumi ilo linatsitsimuka kachiwiri. Woyimira kuweruza, onse a iwo, anakankhira kumbuyo mabuku awo, ndipo anati, “Ndiye ife tikusiya ntchito yathu, chifukwa ngati iwo akuphwaya ufulu wa Konstitushoni uwo, iwo adzaphwaya ena onsewo.”

<sup>87</sup> Kodi inu munazindikira tsiku lina pamene Bishopu wanzeru wachikulire Wachimethodisti uja, zomwe iye ananena za—kunena pemphero lija mu—mu mpingo—mu sukulu? Umenewo sunali Mpingo wa Methodisti. Bishopu amene uja anali wanzeru mokwanira kuti adziwe zimenezo. Limenelo linali gulu lina powona momwe iwo angapitire patali kuti alikakamizire pemphero linalake mu—mu sukulu. Ngati iwo ati apambane pa limenelo, iwo apambana pa linalo mwamsanga basi momwe iwo angathere. Iwo akufufuza mpata uliwonse umene iwo angakhoze. Musati mudandaule, iwo awupeza iwo.

<sup>88</sup> O! Ife tikufuna mtanda. Ife tikumufuna Khristu tsopano pamene ife tingathe! Musati mukopedwe ndi munthu yemwe mwinamwake angakhoze kutumiza—zakudya zambiri kumeneko. Musati mukopedwe kuchokera kwa munthu yemwe angakupatseni inu makina abwinoko kuti muzikweramo, kapena nyumba yabwinoko kuti muzikhalamo, ndi kugulitsa mafulu anu obadwa nawo kwa Khristu. Musati muchite zimenezo! Penyani zomwe inu mukuchita. Nthawizonse muzimutsatira mmodzi uyo yemwe amakopedwa ndipo amayimiridwa kumbuyo ndi Mulungu, yemwe inu mukudziwa chomwe—Mulungu ali ndi iwo. Musati mutsatire kukopa kolakwika. Inde! Chabwino. Musati muyesere kutenga malo a winawake.

<sup>89</sup> Masomphenya pa kachisi, iye anawona pa—pa mpandowachifumu Mulungu atakwezeka pamwamba, Mulungu ali kukwezedwa pamwamba. Tsopano inu mukuona, mfumu iyi yomwe. . . Iye anali atapanga chitsanzo pamaso pa Yesaya, ndipo Yesaya anawona kuti mfumu imeneyo mwamsanga pamene iyo inachoka pa kuyitanidwa kwake—Mulungu anamukantha iye ndi khate. Ndiye Yesaya anaganiza, “Ndiyenera kuchita chiyani ine?” Uziya anali atafa, iye anali atatsamira kwambiri pa nkono wake. Ndipo iye anaganiza kuti iye anali atathedwa; iye akanachita chiyani? Moyo iwo womwe unali utamuchokera mwa iye pafupifupi. Chotero mneneri wamng’ono anachita chiyani? Iye anapanga ulendo wake wopita ku kachisi kuti akapemphere. Iye anagwera pansu pa guwa, ndipo analira mokweza.

<sup>90</sup> Nthawizina Mulungu amalola zozidalira zomwe kuti zigwetsedwe kuchokera pansu pathu. Nthawizina Iye amalola matenda atikanthe ife. Iye amalola zokhumudwitsa, kupweteka kwa mitu, zitikanthe ife. Nthawizina Iye amachita zimenezo kuti akutengere iwe pamene iwe ukanati ukopedwe ndi Uthenga.

Khalani anzeru mokwanira kuti muchigwire icho. Musati mukhale opusa mokwanira kuti muyende kuchoka kwa icho.

<sup>91</sup> Zindikirani, Yesaya anadziwa kuti iye ayenera kuti apeze chinachake chosiyana. Chotero kodi iye anachita chiyani? Iye anapita ku kachisi; iye anakwezera mmwamba manja ake, ndipo iye analirira mokweza kwa Mulungu. Ndipo iye anagwera mu masomphenya. Ndipo pamene iye anagwera mu masomphenya, iye anawona Mulungu, osati ali pa mpandowachifumu pansi pano, koma atakwezedwa mmwamba, mmwamba patali. O, mai! Ulemerero Wake unali kumutsatira Iye ndipo ananyamulidwira mmwamba mpaka ku Miyamba. Ndipo iye anawona mmbuyo ndi mtsogolo kupyola mu kachisiyo, Aserafi akuwuluka. O, mai! *Mserafi* ndipo iye amathanthauza “woyatsa,” mawu oti *Mserafi* amathanthauza. Omwe ali apafupi ndi ku guwa. Makamaka, Aserafi ndi iwo omwe amalandira nsembe, ndipo amamutsuka wopembedza, ndiyeno nkumupereka iye kwa Mulungu, *Mserafi* amachita izo. Tsopano, *Mserafi* uyu anali zokhalapo zaungelo, ndipo iwo ali apafupi kumene kwa Mulungu, pa guwa pomwe. Ndipo iwo amalandira nsembe. Izo zimasonyeza chilungamo cha Mulungu, kuti tchimo silingakhoze kubwera mu kukhalapo Kwake kupatula ilo litatetezedwera. Mwaona? Ndipo Aserafi awa...

<sup>92</sup> Inu mukumbukira mu Mibadwo Isanu ndi iwiri momwe iwo ankatetezera Mauthenga amenewo, mmodzi ku mbali iliyonse? Inu mukukumbukira, ife tinawatengera iwo kubwerera ku munda wa Edeni ali ndi lupanga lamoto atayima pamenepo? Iwo amatetezera guwa.

<sup>93</sup> Ndipo Yesaya, mneneri wamkulu uyo, pamene iye anagwera mu Mzimu, iye anawona choyamba Mulungu atakhala patali Mmwamba, pamwamba pa mfumu iliyonse ya padziko lapansi. Anati, “Ine ndinawona a Mfumu, Ambuye atakhala patali ndipo atakwezedwa pamwamba (ndiye iye anaiwona Mfumu yeniyeni), ndipo ulemerero Wake unali kumutsatira Iye.”

<sup>94</sup> Ndipo iye anawona Aserafi akuwuluka kudutsa mu nyumbayo. Iwo anali nawo mapiko ophimba pa nkhope zawo, mapiko ophimba pa mapazi awo, ndipo iwo anali akuwuluka ndi mapiko awiri. Ndipo iwo anali akufuula, “Woyera, woyera, woyera, Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse! Woyera, woyera, woyera, Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse!” Njotani—nyimbo yotani, kayimbidwe kotani!

Inu mukuti, “Iwo ayenera kuti ankanena izo mopepuza kwambiri. ‘Woyera, woyera, woyera, Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse.’” [M’bale Branham akusanzira—Mkonzi.]

<sup>95</sup> Yesaya anati, “Pamene iwo anali kuyankhula, ziwundo za nyumbayo zinagwedera ndi liwu lawo.”

<sup>96</sup> Iwo sanali akumangoti tsopano, “Woyera, woyera, woyera [M’bale Branham akusanzira—Mkonzi.]” O, ndi liwu lotani.



Ndipo anati, “Ndipo nsanamira zinasuntha ndipo zinagwedera ndi liwu lawo.” Iwo anali akufuula, zinthu zaungelo zimenezo zitayima pafupi ndi pa mbali ya Mulungu, akufuula, “WOYERA, WOYERA, WOYERA ALI AMBUYE MULUNGU WAMPHAMVUZONSE!” Ndi masomphenya otani! Psyii! O, mai!

<sup>97</sup> Zindikirani kachiwiri, Yesaya yemwe anakhala akutsamira pa nkono wa Uziya ndipo anamuwona iye akufa pansi pa chiweruzo cha Mulungu; ndipo kenako anawona zinthu zoyera izi zomwe zinali pafupi ndi ku mbali ya Mulungu, Aserafi akufuula, “WOYERA, WOYERA, WOYERA, AMBUYE MULUNGU WAMPHAMVUZONSE!”...Ndipo Angelo oyera amenewo anaphimba nkhope zawo. Angelo oyera anaphimba nkhope zoyera pamene pali Mulungu woyera, ndiye ndife yani? Ndipo tsopano...

<sup>98</sup> O, inu Amethodisti, ndi Abaptisti, ndi Apresbateria, ndi Achipentekoste, ndife yani? Pamene Angelo oyera amabisa nkhope zawo zoyera pansi pa phiko kuti ayime mu kukhalapo kwa Mulungu, pamene Angelo, cholengedwa chomwe chiri makamaka chopyola Angelo...Angelo samayima pamenepo, Mserafi yekha. Iwo ndi oposa Angelo. Ndipo Mulungu ndi woyera kwambiri mpaka iwo amaphimba nkhope zawo mu kukhalapo kwa Mulungu woyera. Ndipo chinthu chokha chimene iwo akadakhocha kunena chinali, “WOYERA, WOYERA, WOYERA ALI AMBUYE MULUNGU WAMPHAMVUZONSE!” Psyii! Chophimba chapadera cha iwo kuti ayime mu kukhalapo kwa Mulungu...Ndi chophimba cha mtundu wanji chimene ife tikuchisowa? Iwo ankayenera kuti akhale ataphimbidwa.

<sup>99</sup> Tsopano, ine ndikufuna ndinene izi pakali pano: Magazi a Yesu Khristu ali okwanira-zonse. Mukuona? Khristu sikuti anawafera Aserafi amenewo. Ayi, ayi! Koma iwo anali zokhalapo zolengedwa. Iye sanawafere konse Angelo; Iye anawafera ochimwa. Iye sanawafere konse anthu oyera; iye anawafera osayera. Ndipo pamene inu mukuganiza kuti ndinu woyera, Iye sanakuchitireni inu ubwino uliwonse. Koma pamene inu muzindikira kuti sindinu kanthu, ndiye Iye anakuferani—Iye anakuferani inu. Mwaona? Pamene inu muzindikira kuti sindinu kanthu, ndiye Iye ali Mmodzi—inu munali mmodzi yemwe Iye anakuferani. Mulungu ali yense woyera. Palibe kalikonse kwa Iye koma chiwero; ndizo zonse, ungiwiro.

<sup>100</sup> Tsopano, tiyeni tiwazindikire mapiko awa kwa maminiti pang’ono. Ife tikupeza kuti mapiko awiri iye ankaphimbira nawo nkhope yake. Mai, taganizani! Ngakhale Angelo oyera ankaphimba nkhope zawo zoyera mu kukhalapo kwa Mulungu woyera. Ndipo chinthu chokha chimene iwo akanakhocha kumanena chinali, “Woyera, woyera, woyera ali Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse! Woyera, woyera, woyera Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse!” Ndipo ife tikuwuzidwa kuti

iwo ankafuula usana ndi usiku. Ndiyo sitepe yoyamba kuchokera kwa Mulungu kubwera mmusi. Usana ndi usiku, opanda kulekeza. Ndipo inu mukuganiza kuti ife timapanga phokoso lambiri. Inu mukuganiza chiyani za mamilioni a amenewo atazungulira mpandowachifumu ali ndi liwu limene linagwedeza ziwundo za kachisi pamene mmodzi yekha wa iwo anafuula, “Woyera, woyera, woyera”? Inu mukudziwa, liwu lake linagwedeza kachisi, pamene mamilioni a iwo akufuula pozungulira mpandowachifumu wa Mulungu. “Woyera, woyera, woyera, woyera, Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse! Woyera, woyera, woyera, woyera, Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse,” ali ndi mapiko ophimba pa nkhope zawo, mapiko ophimba pa mapazi awo, ndi mapiko mwa kulemekeza, ulemu. O, mai!

<sup>101</sup> Tsopano palibe kulemekeza kapena maulemu kwa chirichonse chimene chimakamba za chiyero. Iwe ukayankhula za chiyero, iwe umatchedwa woyera wodzigudubuzwa. Palibe kulemekeza, palibe maulemu kwa ngakhale Mulungu, anthu Ake, kapena Mawu Ake.

<sup>102</sup> Tsopano, kodi gulu ili lipita kukathera pati? (Ine ndikuganiza iwe ukulondola, Ben. Iwe unamenya msomali pa mutu nthawi imeneyo, Mwananga. Inde, ndizo pafupi kulondola.) Kodi gulu losalemekeza ili lidzakathera kuti ndiye? Kodi gulu losalemekeza ili lidzakathera kuti (ndi zimenezo!), iwo amene alibe kulemekeza nkomwe kwa Mulungu.

<sup>103</sup> Inu mukudziwa, izo zinkakhala kuti ngati mkazi kapena mwamuna akananena kuti iwo anali Akhristu, anthu ankalemekeza icho; koma lero iwo amangokonda kufuna kuwona kuti ndi kuseka kochuluka chotani kumene iwo angakhoze kupanga pa icho. Mwaona? Gulu losalemekeza! Mai! Chifukwa chiyani? Inu mukudziwa chiyani? Ichi ndi chifukwa chake. Iwo sakuzindikira kuti icho ndi Choonadi. Iwo sakuzindikira za Mulungu. Iwo sali kukumbukira kuti Baibulo limanena, “Kuti Angelo a Mulungu amamanga misasa pozungulira iwo amene amamuwopa Iye.” Iwo samangobwera kokha ndi kudzawachezera iwo; iwo—iwo amazika mahema awo pansi. Amen! “Angelo a Mulungu amamanga misasa pozungulira iwo amene amawopa Dzina Lake.” Iwo amakhala pamenepo usana ndi usiku.

M'bale wachikulire wachikuda anayimba nyimbo imeneyo, *Angelo Amakhala Akuyang'anira Pa Ine*. Anati,

Usana wonse usiku wonse Angelo amakhala  
akuyang'anira pa ine. . .

<sup>104</sup> Ndiko kulondola. Usana wonse ndi usiku wonse, Angelo amakhala akuyang'anira pa ine. Yesu ananena za aang'ono awa, anati, “Khalani osamala kuti musati muziwakwiyitsa mmodzi wa iwo, chifukwa Angelo awo nthawizonse amawona nkhope ya Atate Anga omwe ali Kumwamba.” Mwaona? Iwo

nthawizonse amamanga msasa pozungulira, kuwayang'anira amenewo. Ndipo iwo sikuti amakhulupirira konse zimenezo, anthu opanda umulungu. Ife tifika poti titenge pa chimene umulungu ndi kupanda umulungu ziri mamawa, ngati Ambuye alola.

<sup>105</sup> Tsopano zindikirani, iwo sikuti amakhulupirira konse zimenezo. Iwo ataya khalidwe lonse, maulemu onse, kulemekeza konse, ndipo komabe amapita ku mpingo. Gulu lopanda kulemekeza kwambiri lomwe liripo, ndi iwo amene amapita ku mpingo. Ndiko kulondola.

<sup>106</sup> Wogulitsa mowa wachikulire, wakachasu, akubwera uko pa msewu, akudutsa mozungulira, ndipo ataledzera mwatheka, iwe ukayankhula ndi iye zokhudza Ambuye, iye angayime ndi kuyankhula kwa iwe. Ena a iwo a nsana wa ndele, otchedwa okhulupirira, ziwalo za mpingo, angakuseke mu nkhope yako kumene, chifukwa iwo samafuna...?....Ndithudi! Iwo ndi opanda kulemekeza. Inu mukuganiza kuti iwe uyenera kukhala wa kalankhulidwe kawo kakang'ono kapena iwe suli ngakhale kukhala ku mbali yawo ya msewu. Mwaona? Ndi choonadi. Kusalemekeza.

<sup>107</sup> Tsopano, Angelo awa, pamene iwo ali mu kukhalapo kwa Mulungu, iwo anali...Amakhulupirira izo...Davide anati (inu mukukumbukira ife tinali nawo kuno mausiku angapo apitawo pamene ine ndinali kulalikira pa chinachake), ndipo iye anati—Davide anati, “Ine ndimawayika Ambuye nthawizonse patsogolo panga, kuti ine ndisati ndidzasunthidwe. Moonjezerano,” iye anati, “ndiye pamene ine ndichita zimenezo, thupi langa likhala likupuma mu chiyembekezo.” Inde, bwana! “Chifukwa ine ndikudziwa chimene...Iye sadzasiya moyo wanga mu hade, ngakhale kulola Woyera Wake Mmodzi awone chivundi. Pakuti Ambuye ali nthawizonse patsogolo panga.”

<sup>108</sup> Kulikonse kumene inu mupita, ikanipo Mulungu. Ngati munthu ayamba kukwiya nakutukwanani inu, ikani Mulungu pakati pa inu ndi iye. Ngati munthu akutchani inu woyera wodzigudubuza, ikani Mulungu pakati pa inu ndi iye. Ngati akazanu ayamba kukwiya nanu, ikanipo Mulungu. Ngati amunanu ayamba kukwiya, ikanipo Mulungu. Ngati ana akuwawitsani inu, ikanipo Mulungu. Mwaona? Chirichonse chimene inu muchita, ikanipo Mulungu. Ngati bambo ndi mayi akupatsani inu kakhofi kakang'ono ndi kukukonzani inu, ikanipo Mulungu. Kumbukirani chimene Mulungu ananena chokhudza zimenezo? “Mulereni mwana mwa njira imene iye ayenera kuyendamo.” Mwaona? Nthawizonse muzikumbukira, ikanipo Mulungu. Ikani Mulungu patsogolo panu, ndipo inu mudzakhala nako kulemekeza kwa Mulungu ndi ulemu kwa Iye. Ndiko kulondola.

109 Tsopano penyani! Mapiko awiri iye anaphimba nkhope yake ndipo mapiko awiri. . . Zimenezo zinkatanthauza, kulemekeza, kulemekeza pamaso pa Mulungu, anawerama—anaphimba nkhope yake. Tsopano, ife—ife sikuti tiri nawo mapiko aliwone kuti tiziphimbira nawo nkhope zathu, ife timaweramitsa mutu wathu pa mapazi Ake, kuweramitsa mitu yathu ndi kupemphera mwa kulemekeza, ulemu. Inde bwana! Kuzindikira izo. Ndi mapiko awiri iye anaphimba mapazi ake. Mapazi ake. . . Anaphimba, mapazi ake—zinkayimira kudzichepetsa ndi kulemekeza.

110 Monga Mose, Mose mu—ulemu wa Mulungu akumuwuzwa iye kuti iye anali pa malo ojera, iye anavula nsapato zake. Mwaona? Iye anachita chinachake ku mapazi ake. Paulo mwa ulemu kwa Mulungu, kulemekeza. . . Pamene Mngelo wa Ambuye anabwera pamaso pa iye mu Lawi la Moto limene lija, iye anagwera pansu pa nkhope yake. Ulemu! Yohane Mbatizi, iye anali nawo ulemu woterowo pamene iye anamuwona Yesu akubwera, iye anati, “Ine sindine woyenera nkomwe kuti ndigwire mapazi Ake.” Mwaona? Mapazi, kusonyeza ulemu. Mwaona?

111 O! Khalani ozindikira, pano pali chinthu chimodzi chokha choti uzikhala ukuchizindikira: kuchepa kwako. Ngati iwe ukufuna kuti ufike penapake ndi Mulungu, dzipange wekha wamng’ono kwenikweni. Usati udzipange wekha wamkulu monga Uziya. Iye analowa mkati mmenemo, ndipo iye—iye anati, “Ine ndichita izi mulimonse, kaya ine. . . Inu mulibe ntchito yoti mundiwuzwe ine.” Mwaona? Iye akanati adzipange yekha modzichepetsa. “Inde, Antchito a Khristu, ndikhululukireni ine.” Iye sakanatenga konse khathe. Ayi! “Ine ndikudziwa iyo ndi ntchito yanu; Mulungu anakuyitanani inu. Uwo ndi udindo wanu. Inu mupitirire ndikumachita izo, Mabwana. Ndine wopepesa kwambiri.” Akanati achokepo, bwezi muli kulemba kosiyanana mu Bukhu ili. Koma pamene iye anakonzedwa, iye anakhala wokwiya.

112 Iwe ukamawakonza anthu za chinachake kapena kuwawuzwa iwo za zochita zawo zolakwika, iwo amasiya mpingo. Iwo amafuna. . . ukapita kwa winawake, kukawawuzwa akazi kuti iwo asamavale tsitsi lalifupi, “Chabwino, ine ndipita kwinakwake kumene iwo angakhoze kulivala ilo.”

113 Mkazi anapita kuno nthawi ina kalelo. . . ine ndinamutumiza mkazi wanga kumeneko. Ife tinali mu msonkhano; iye analibe nthawi yoti atsuke tsitsi lake, ndipo iye. . . ine ndinamuwuzwa iye kuti apite ku imodzi ya mashopu okongoletsa ndi kukatsukitsa tsitsi lake. Iye anapita kumeneko, ndipo mkazi ameneyo sanali kudziwa nkomwe momwe angalidzutsire tsitsi lakelo. Iye anachita kulipotera ilo pamwamba pa mutu wake. “Taonani,” anati, “Ine sindinayambe ndatsukapo tsitsi la aliyense—wokhala ndi tsitsi lalitali.”

Iye sankadziwa kalikonse za izo. Ine sindikudziwa. O, mai! Mwaona?

114 Iwo sadziwa kuti Izo zonse ndi chiyani. Chifukwa chiyani? Ndi chifukwa cha maguwa ofooka omwe iwo akhala akukhala pansu pake (chimodzimodzi!), maguwa ofooka omwe sangati awauze Choonadi. Iwo amanyengerera nazo Izo. Mwaona? Kulibwino... Izo zikanakhala bwinoko ngati inu mukunachimva icho... Ndipo iwe ukati uyankhule kwa mmodzi wa iwo, iwo ayimirirapo, ndi kufufuma, ndi kuti, "Ine sindizamumvetsera konse woyera wodzigudubuza uja kachiwiri." Mwaona? Pitirira nazo, Uziya. Ndiko kulondola!

115 Khate, bwanji, ine kunalibwino ndikhale ndi khate nthawi iliyonse kusiyana ndi khate la mtundu umenewo; chabwino, ilo ndi khate la solo. Mwaona? Pamene iwe upita mmwamba ndi kukayamba... Iwe uli apo pomwe nkuyambanso ndi khate—tchimo, lomwe liri loyipitsitsa kuposa khate. Ndi khate la mu solo.

116 Uziya mwinamwake anapita ndipo anagona ndi makolo ake Baibulo linatero. Chomwe iye anali wopulumutsidwa, chifukwa iye anangochita chinachake cholakwika. Koma pamene iwe uchita icho, ukudziwa bwinoko, ndiye iwe umayamba khate la solo. Ndiyeno palibe njira yoti utengere solo ya khate mkati; inu mukudziwa zimenezo.

Kotero ndiye, dzipangeni inueni kuchepa. Dzichepetseni pamaso pa Mulungu...?... Musati muyambe kuzitukumula nonse ndi kufufuma; fufuzani Malemba ndi kuwona ngati ziri zolondola.

117 Ine ndinamuwuza winawake osati kale litali... Iwo anati, "M'bale Branham, ine ndamva kuti ndinu a Yesu Yekha?"

Ine ndinati, "Inu munamva molakwika." Mwaona? Ine ndinati, "Sindine wa Yesu Yekha."

Anati, "Chabwino, inu mumabatiza mu Dzina la Yesu."

118 Ine ndinati, "Zimenezo sizikundipanga ine wa Yesu Yekha." Ine ndinati, "Chiphunzitso cha Yesu Yekha; iwo amabatizira ku kusintha. Ine sindimakhulupirira mu zimenezo. Ine sindiri kukhulupirira kuti mwamsanga pamene iwe wabatizidwa mu Dzina la Yesu zimakuchotsera solo yako—machimo ako; ine ndimakhulupirira Petro anati, 'Lapani choyamba; tembenukani chozungulira, inu munaphonya mzere; pitani kumbuyo.'" Kalapeni ndiyeno mukasonyeze kwa dziko kuti inu mwakhala—inu ndinu wobatizidwa. Ine ndimakhulupirira izo... Ine sindimakhulupirira zakuti kubadwa kachiwiri kuti ndiwo ubatizo wa Mzimu Woyera. Iwo siuli ubatizo wa Mzimu Woyera; uko kwangokhala kubadwanso kwachiwiri. Ife timabadwanso ndi Magazi. Selo ya Magazi imabwera kuchokera—ine ndikutanthawuza, selo ya moyo imabwera kuchokera ku Magazi. Iwe umabatizidwa ndi Mzimu Woyera kulowa mu thupi, koma

iwe umabadwa ndi Magazi. Mwamtheradi. Iwe umabadwa ndi magazi a abambo ako. Ndine wobadwa kachiwiri ndi Magazi a Abambo anga, ndi mwa anu—Abambo athu, Khristu. Inde, bwana!

<sup>119</sup> Koma inu mukuona, ife sitimakhulupirira zinthu zimenezo. Chifukwa ife timabatiza mu Dzina la Yesu Khristu, sikuti zimatipanga ife a Yesu Yekha; osati konse. Ayi, bwana!

<sup>120</sup> Inde, bwana! Mose anadzichepetsa iyeyekha mu kukhalapo pamene iye anamva liwu lija la Mulungu likuchokera pamenepo monga choncho, anati, “Vula nsapato zako.” Mose anafikira pansi ndipo anagwedeza nsapato zake kuzichotsa. Mwaona? Ndiko kulondola.

<sup>121</sup> Paulo, pamene Kuwala kuja kunamukanthira iye pansi. . . Iye anati, “Saulo, Saulo, nchifukwa chiyani iwe ukundizunza Ine?”

Anati, “Ambuye, Ndinu Yani?” Mwaona, pansi pa nthaka pamene. “Ndi ndani ameneyo?”

Anati, “Ine Ndine Yesu (Lawi la Moto lija)—Ine Ndine Yesu. Ndi kovuta kuti iwe uzimenyana ndi zisonga.”

Anati, “Ambuye, kodi ine ndiyenera kumachita chiyani?” Iye anali wokonzeka.

<sup>122</sup> Yohane M’batizi anamuwona Iye akubwera. Mmodzi wa anthu aakulu. . . Yesu anati sipanayambe pakhala pali munthu wobadwa mwa mkazi wamkulu monga Yohane. Ndipo pamene Yohane anamuwona Iye, iye anazindikira kuti iye anali wamng’ono kwambiri, iye anati, “Ine sindiri woyenera kuti ndichotse nsapato Zake.” Amen!

<sup>123</sup> Nthawizonse muzizindikira, munthu wamkulu amadzichepetsa yekha. Njira yopitira kumwamba ndi kutsika, nthawizonse. Dzipangeni inueni wochepa, ndipo Mulungu adzakubweretsani inu mmwamba. “Iye amene adzikuza yekha, adzachepetsedwa, koma iye amene amadzichepetsa iyeyekha adzakwezedwa.” O mai, ine ndimakonda zimenezo.

<sup>124</sup> Dzipangeni nokha wamng’ono; nthawizonse khalani wamng’ono. Musati mukhale wolemera wamkulu; mukhale munthu wamng’ono. Mwaona? Mulungu ndi Mmodzi yekhayo pakati pa ife yemwe ali wamkulu mulimonse. Ndiko kulondola.

<sup>125</sup> Inu simumafuna kuti muziti, “Ndi mpingo woyera, anthu oyer.” O, ayi! Ndi Mulungu woyera (ndiko kulondola) ndi mpingo wosayera ndi anthu osayera. Ndiko kulondola. Palibepo chinthu chotero monga mpingo woyera; ndi Mulungu woyera mu Mpingo. Si anthu oyer; ndi Mzimu Woyera mwa anthu. Ndiye iwe ukuyankhula osati za anthu; iwe ukuyankhula za Mzimu Woyera umene uli mwa anthu. Amen, ameni! Ndiwo mawu oyenera! Amen! Chimenecho chinakhudza pachimake; ine ndinachimverera chimenecho! Inde, bwana! Iye wachikonda

chimenecho; ine ndikudziwa zimenezo. Ulemerero! Inde, bwana! Chabwino.

<sup>126</sup> Dzipangeni nokha wamng’ono. Iye anaphimba nkhope yake ndi awiri, kulemekeza. Iye anadzichepetsa yekha pa kuphimba mapazi ake. Tsopano chachitatu, ndi awiri iye anali kuwuluka. Iye anadziyika yekha mu kuchitapo ndi awiri a iwo. Iye anali wolemekeza pamaso pa Mulungu. Iye anali wodzichepetsa pamaso pa Mulungu. Osati kokha chokhacho, iye sanali atangokhala pamenepo, koma iye anadziyika yekha mu kuchitapo. Kunena za Mpingo. Ameni! Anadziyika yekha mu kuchitapo. Chirichonse chimene iye anali nacho, iye anali wokonzeka kuti apite nacho icho. Inde, bwana! Chinthu chokha chimene iye akanakhoza kunena chinali, “Woyera, woyera, woyera ali Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse;” koma iye anadziyika iyeyekha mu kuchitapo ndi zimenezo. Ndiko kulondola! Iye anafika mu kuchitapo. Ndicho chimene mpingo ukusowa usikuuno, chiripoyamba kukhala wolemekeza, chinthu chotsatira, kukhala wodzichepetsa, ndiye dzitengereni inunokha mu kuchitapo. Inde, bwana!

<sup>127</sup> Iye anamusonyeza mneneri... Pamene Iye anamusonyeza mneneri momwe Iye ankawayimira antchito Ake, momwe Iye ankati adzachtire, kodi mwamuna uyu anachita chiyani, Mngelo uyu? Mneneri uyu anawona liwu lake likugwedeza mizati mu kachisi pamene iye anafuula. “WOYERA, WOYERA, WOYERA, AMBUYE MULUNGU WAMPHAMVUZONSE.” Ndipo nyumbayo inagwedezeka, ndipo... Iye anafuula kachiwiri, “WOYERA, WOYERA, WOYERA, AMBUYE MULUNGU WAMPHAMVUZONSE,” ndipo nyumbayo inagwedezeka.

<sup>128</sup> Yesaya anati, “Watsoka ndi ine!” Mneneri, mneneri wotsimikiziridwa, wobadwa ali mneneri, mneneri wamkulu wa m’Baibulo; ndipo iye anati, “Watsoka ndi ine, pakuti maso anga awona ulemerero wa Mulungu.” Tayang’anani pa mneneri ameneyo akudzichepetsa yekha, mneneri, mwamuna yemwe Mawu a Mulungu anali kubwerako. Koma pamene iye anawona masomphenya ali mu kuchitika, iye anati, “Watsoka ndi ine, pakuti ine ndiri kuyima pafupi kwambiri mpaka ine ndikuwona Kukhalapo kwa Ambuye.”

<sup>129</sup> Anthu athu amakono Achimereka akhoza kuwona zimenezo, ndi kuchokapo, ndi kumaseka pa izo. Ndiko kulondola.

<sup>130</sup> Pamene iye anawona masomphenya ali nkuwonetseredwa, masomphenya owonetseredwa (o Mulungu, chitirani chifundo pa dziko lochimwa ili!)—masomphenya owonetseredwa, iye anafuula mokweza, “Watsoka ndi ine, pakuti ndine munthu wa milomo yosayera, ndipo ine ndimakhala pakati pa anthu a milomo yosayera. Ndine yense wothedwa; palibe chirichonse chabwino pa ine.”

<sup>131</sup> Chabwino, inu mukuti, “Mulungu adalitsidwe, ine ndine wa Presbateria, Methodisti, Baptisti, Chipentekoste; ine sindikusowa kuti ndikhale ndi kumamvetsera ku zinthu zoterozo.” Ndi kusiyana bwanji kulipo, kusiyana bwanji.

<sup>132</sup> Ndipo inu mukukumbukira, mneneri uyu, anayitanidwa kuchokera pa kubadwa kwake, ndipo anatsimikiziridwa, wokonedweratu ku udindo wake, ndipo anali akufunafuna Choonadi, ndipo iye anali atakhala ndi mfumu. Iye anali atawona ntchito za Mulungu ziri kuwonetseredwa, koma pamene masomphenya otseguka anabwera, mmalo mwa kumukweza iye, iye anati, “Watsoka ndi ine. Ndine yense wothedwa. Ine ndalowamo umo tsopano, pakuti maso anga awona ulemerero wa Mulungu.”

<sup>133</sup> Ndipo ife tikhoza kuwona ulemerero wa Mulungu, ndipo ife timapita mozungulira ndi kumati, “Gulu la oyera odzigudubuza, anthu omwe ali openga.” Palibe chodabwitsa kuti ife sitikufika kulikonse.

<sup>134</sup> Tsopano kumbukirani, ine ndinakuwuzani inu kuti pamene ine ndinafika kuno kuti ndinena chinachake, icho chidzawathandiza anthu. Inde, ife tiyenera kukhala—ochilemekeza Icho. Ife tiyenera basi kuchipatsa icho kugunda kulikonse kwa ulemu kumene ife tingakhoze, pamene ife tiwona masomphenya otseguka ochokera kwa Mulungu akuyankhula pamenepo, ndi kudziwa kuti ndi Choonadi.

<sup>135</sup> “Watsoka ndi ine,” anatero Yesaya. “Ine ndiri mu chipinda muno usikuuno (kapena lero kapena lililonse pamene izo zinali), ndipo ine ndikuwona ulemerero wa Mulungu. Ine ndikumuwona Mngelo akuyankhula, ndipo ine ndikuwona chinachake chikusuntha. Ndipo ine ndikuyang’ana pamwamba apo, ndipo ine ndikumuwona Mulungu akuwonetseredwa pomwe pano. Watsoka ndi ine, chifukwa ndine munthu wa milomo yosayera, ndipo ine ndimakhala pakati pa anthu osayera.”

<sup>136</sup> Penyani chimene chinachitika. O, kodi Iye anachita chiyani? Iye anamusonyeza—Yesaya mneneri kuti munthu adzakhala wolemekezeka, adzakhala wolemekeza mu kukhalapo Kwake. Kulemekeza, ndi kudzichepetsa, ndiyeno nkulowa mu kuchitapo. Ndiko kulondola! Kufika mu kuchitapo.

<sup>137</sup> Monga mkazi pa chitsime, pamene iye anawona chinachake chikuchitika, m’bale, iye anali ndi mapiko awiri. Iye anachokapo ndi iwo mwamsanga kumene. Iye anafika kunjira uko pa chitsime cha Yakobo kuti adzatunge ena a madzi okhathamira aja omwe iwo anali kutsutsanira; koma pamene iye anafika pa kumwa kuchokera pa Kasupe Wamoyo uja, iye anapita mu kuchitapo mwamsanga ndithu. Iye sanati, “Bwana, chonde ndiwuzeni ine kumene inu munapeza maphunziro anu. Kodi inu munazipeza kuti zinthu zimenezi? Inu munaziphunzira motani izo?” kapena,



“Inu munadziwa motani kuti ine ndinali nawo amuna asanu? Inu munadziwa bwanji chomwe chinali cholakwika ndi ine? Inu munadziwa bwanji kuti ine ndinali mkazi wa ku Samaria? Inu munadziwa motani zinthu izi?” Iye sanafunse konse; Iye anati, “Bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndinu Mneneri. Ife tikudziwa pamene Mesiya adza, Iye adzatiwuza ife zinthu zimenezi.” O, mai! Iye anachizindikira icho mwa Lemba. Ndiyeno iye anati, “Ine ndikudziwa kuti pamene Mesiya adza, Iye adzatiwuza ife zinthu zimenezi.”

Iye anati, “Ine ndine Iye.”

<sup>138</sup> Iye anapita mu kuchitapo. Mpaka mu mzinda momwe iye anapita zolimba momwe iye akanathera kupita; anati, “Bwerani, mudzamuwone Mwamuna Yemwe wandiwuza ine zinthu zimene ine ndazichita. Kodi uyu si Mesiya amene!” Pamene iye anawona Choonadi, iye sanati ayesere kuwutenga mpirawo, iye—koma iye anali wotsimikiza kuwupatsa Iwo wina—wina—ulemu wochuluka. Ndipo iye anali motsimikiza kuwapatsa Iwo thandizo lochuluka, chifukwa iye anapita pansu mu mzinda ndipo anati, “Inu, bwerani mudzaone. Ngati inu simukukhulupirira izo, tiyeni, mupite ndi ine.” Ulemerero!

<sup>139</sup> Ine ndikumverera monga woyera wodzigudubuza usikuuno. Inde, bwana! Mai, ngati ndiyo njira imene inu mukumverera kukhala woyera wodzigudubuza, ndiroleni ine ndikhale mmodzi. Inde, bwana! Ine ndikudziwa kuti Iye akulondola. Ine ndikudziwa Iye ali pano. Ine ndikudziwa Mesiya yemwe uja, ine ndikudziwa Mulungu yemwe uja, Khristu yemwe uja, ali pomwe pano mu nyumba yaying’ono yakale yotentha iyi usikuuno. Ine ndikhoza kutsimikizira izo kwa inu. Amen!

<sup>140</sup> Tamuonani Mngelo uyo wa Ambuye ali mu ngodya pa mwamuna yemwe wakhala apayu. Dzina lake ndi... Iye ndi m’busa. Bambo Witt. Iye ndi wochokera komwe ku Virginia (kulondola!) akuvutika ndi kusokonezeka kwa mitsempha. Ngati inu mukhulupirira ndi mtima wanu wonse, inu mukhoza kupita kwanu ndi kukakhala muli bwino. Kodi inu mukhulupirira zimenezo, bwana? Chabwino, pitani kwanu ndipo mukakhale bwino; kusokonezeka kwa mitsempha yanu kwatha.

<sup>141</sup> ...?...ali apo pomwe; dzina lake ndi Morriah. Iye akuchokera ku Illinois. Iye ali ndi vuto la thumbo. Ngati inu muti mukhulupirira izo, bwana... Kodi inu mukukhulupirira izo? Ndine mlendo kwa inu. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Izo zikusiyani inu. Aleluya!

Pamene khala la moto linamukhudza mneneri,  
Kumupanga iye wangwiro monga wangwiro  
akanakhallira;

Pamene Liwu la Mulungu linati, “Ndati ati atipitire Ife?”

Ndiye iye anayankha, “Ine ndiri pano; nditumeni ine!”

<sup>142</sup> Ziribe kanthu chomwe kuzunzidwako kuli, ziribe kanthu chomwe mtandawo uli, “Nditumeni ine, Ambuye; ine ndiri pano!” Ziribe kanthu angati omwe ati akukane iwe, ndi angati *awa, awo*, kapena *ena*, “Nditumeni ine!”

<sup>143</sup> Iye ali Mesiya yemwe uja. Iye ali pomwe pano tsopano. Ine ndikumuwona Iye kachiwiri. Amen! Ndi chiyani chimenecho?

<sup>144</sup> Mkazi ameneyo anapita mu kuchitapo. Iye anatenga mapiko amenewo ndipo anayamba kuwuluka. Iye analowa mu kuchitapo mwamsanga kumene.

<sup>145</sup> Pamene Mtumwi Petro, pamene iye anamutenga Mulungu pa Mawu Ake tsiku lina kujaku ku nyanja. . . Iye anali ataweza usiku wonse ndipo anali asanagwire kalikonse. Ndipo Yesu anadza kwa iye; Iye anati, “Ponyera nkhoka yako ku mbali ina ya ngalawayo.”

<sup>146</sup> Iye anati, “Ambuye, ndine nsodzi; ine ndimadziwa pamene izo zikudyera ndi pamene izo sizikutero. Ine ndimadziwa kumene izo ziri ndi kumene izo kulibe. Koma ine ndaweza usiku wonse ndipo ine sindinagwire ngakhale kathemba. Tsopano, ngati Inu mukuti ponyera cha uko. . . Ine ndikudziwa kuti kulibe nsomba kumeneko, koma pa Mawu Anu, Ambuye, ine ndikupita kukayala pansipo nkhoka.” Kodi iye anachita chiyani? Iye anapita mu kuchitapo. Amen!

<sup>147</sup> Pali dziwe lodzaza madzi pano. Ngati inu simunayambe mwabatizidwapo mu Dzina la Yesu, ndi nthawi yoti mulowe mu kuchitapo. Ngati ndinu membala chabe wa mpingo ndipo simukumudziwa Mulungu mwa ubatizo wa Mzimu Woyera, ndi nthawi yoti mulowe mu kuchitapo. Kulondola? Phimbani nkhope yanu mwa kulemekeza. Phimbani mapazi anu mwa kudzichepetsa, ndipo weramitsani mabondo anu ndi kupita mu kuchitapo. Ngati inu simukumudziwa Mulungu, pitani mu kuchitapo.

<sup>148</sup> Pamene munthu wakhungu yemwe sankakhoza kupenya, pamene Yesu anayankhula kwa iye, ndipo analavulira pa timatope, ndi kuwayika iwo mu maso ake, ndipo anafika kwa iye kuti amuchiritse—kuchiritsa. Pamene iye anatero, iye anapita mu kuchitapo. Iye anafalitsa kutchuka Kwake. Iye sanayesere kuti awutenge mpirawo; koma m’bale, iye anafalitsa kutchuka Kwake kupyola ku zigawo zonse zozungulira kumeneko. Kodi iye anachita chiyani? Iye anafika mu kuchitapo.

Nthawi ina munthu wakhungu anachiritsidwa ndipo anati. . .

“Munthu ameneyo ndi wochimwa. Iwe sukumudziwa nkomwe Iye!”

149 Iye anati, “Kaya Iye ndi wochimwa kapena ayi, ine sindikudziwa; koma chinthu chimodzi ichi ine ndiri kuchidziwa, pamene ine poyamba ndinali wakhungu, ine ndikukhoza tsopano kupenya.” Kodi iye anachita chiyani? Iye anafika mu kuchitapo.

150 Ndicho chimene mpingo ukusowa. Kufika mu kuchitapo! Ife takhala nawo mawonekedwe ambiri, ife takhala nawo upamwamba wa chidziko wochuluka; ife tikusowa kuti tilowe mu kuchitapo. Amen! Iye anafalitsa kutchuka Kwake kunjja kulikonse.

151 Anthu pa Pentekoste, iwo sanali kudziwa zochuluka kwambiri. Iwo sankakhoza kulemba maina awo omwe, ena a iwo. Iwo ankachita mantha. Iwo analowa mu chipinda chapamwamba. Koma tsiku lina kodi iwo anachita chiyani? Iwo anapita mmwamba umo mwa kumvera ku Mawu Ake. Iwo anatenga Mawu Ake. O, ngati anthu lero atangotenga Mawu Ake, ndiye iwo afika mu kuchitapo. “Dikirani inu mu mzinda wa Yerusalemu.” Luka 24:49.

“Inu mudzalandira Mzimu Woyera zitachitika izi lonjezo—zitachitika izi Mzimu Woyera udzabwera pa inu; ndiye inu mudzakhala mboni kwa Ine.” Machitidwe 1:8.

152 Luka 24:49 amati, “Taonani, Ine ndidzatumiza lonjezo la Atate pa inu: koma kadikireni mmwamba ku mzinda wa Yerusalemu kufikira inu mutadzazidwa ndi mphamvu yochokera kumwamba.” Motalika bwanji? Ora limodzi, maora awiri, masiku khumi, miyezi inayi, miyezi isanu ndi umodzi, sizinapange kusiyana kulikonse. Kufikira! Ndi motalika bwanji zimenezo? Basi kufikira. Pamene iwe umufunsa Mulungu pa chirichonse, khala pomwepo kufikira. Amen! Khala kufikira. Kufikira chiyani? Kufikira izo zitachitika. Dziyitanireni izo! Khulupirani izo! Gwiritsitsani kwa izo! Pitani mu kuchitapo! Chitirani umboni za izo! Chitirani umboni! Musati muzichita mantha. Fikani mu kuchitapo!

153 Iwo anali mu chipinda chapamwamba akutani? Akuyamika ndi kudalitsa Mulungu. Chifukwa chiyani? Lonjezo; iwo ankadziwa kuti izo zinkayenera kuchitika. Ndi inu pamenepo; fikani mu kuchitapo. Yambani kumuyamika Mulungu kufikira Lonjezo litakwaniritsidwa. Inu muli nalo lonjezo.

154 Ngati inu mukukhulupirira kuti Mulungu amachiza, khalani mu kuchitapo. Ngati inu mukukhulupirira kuti Iye akutchulani inu apo tsopano, ndipo inu mukugwiritsabe kwa Iye, khalani mu kuchitapo. Amen! Khalani mu kuchitapo! Inu muli nawo mapiko awiri, kotero agwiritseni ntchito iwo. Khalani mu kuchitapo! Akupizeni iwo mmbuyo ndi mtsogolo. “Ambuye, ine ndikukhulupirira; Ambuye, ine ndikukhulupirira.” Inu simungakhoze kumangofuwula, “Woyera, woyera, woyera”; inu

muyenera kunena, “Ambuye, ine ndiri kukhulupirira!” Khalani mu kuchitapo! Ameni!

<sup>155</sup> Iwo anakhala mu kuchitapo kufikira uko kunabwera nkokomo wochokera Kumwamba wonga mphepo ya mkuntho yamphamvu. Ndiye pamenepo panali kuchitapo kwenikweni. Ndiye iwo analowa mu kuchitapo.

<sup>156</sup> M’bale, mlongo, chimene ife tachiwona chikuchitika mu masiku otsiriza ano chinayenera kutiyika ife mu kuchitapo. Ameni! Ife tiyenera kukhala mu kuchitapo. Ndiko kulondola chimodzimidzi. Ife timakhala pozungulira ngati kuti chinali chinachake. . . Ndipo chabwino, anthu amakhala pozungulira, anthu Achipentekoste; Ambuye akachita chinachake; iwo amati, “Unhu! Izo ndi zabwino kwambiri.” O, mai! Siziri kuwoneka mochuluka kwambiri monga Mserafi yemwe amakhala pafupi ndi Mulungu. Ndiko kulondola. Mtumiki, amene ali ngakhale wapafupi kwa Mulungu. Inu mumakhala mwana Wake mopitirira kupyola guwa lamkuwa.

<sup>157</sup> Aserafi ali pa guwa lamkuwa. Koma inu ngati mwana wamwamuna kapena wamkazi mumapita mpaka mu kukhalapo kwa Mulungu. Inu simusowa kuti muzipita kupyolera mwa wansembe aliyense ndi zinthu zina zonse izi. Iye ndiye Wansembe wanu. Mwaona? Apo pomwe mu kukhalapo Kwake monga ana aamuna ndi aakazi. M’bale, ine ndikukhulupirira ife tiri ndi zoposa mapiko awiri. Ameni! Ife tiri ndi Mzimu Woyera! Ndiko kulondola.

<sup>158</sup> Koma ife tiyenera kukhala mu kuchitapo ndi kulemekeza ndi kudzichepetsa, osati mu kuchitapo kuyesera kuti ukankhire chinachake pa winawake, koma ndi kulemekeza koteroko ndi kudzichepetsa kuti ife tikhoza kupita mu kuchitapo ndi kuti, “Atsoka ndi ife, ife takuwona Kukhalapo kwa Wamphamvuzonse. Ife tawaona masomphenya akuchitika, basi zimene Iye ananena. ‘Ntchito zimene Ine ndikuchita, mudzazichita inu izonso. Zoposa izi inu mudzazichita, pakuti ine ndikupita kwa Atate Anga.’”

<sup>159</sup> Ife taziwona zambiri zikuchitika zomwe sizinalembedwe nkomwe mu. . . Chabwino, ife tikuwona zambiri zikuchitika mu msonkhano umodzi ndi zinthu zimenezo zoposa zimene zinalembedwa mu Baibulo. Ndiko kulondola. Zochuluka mu msonkhano umodzi kuposa zimene zinalembedwa mu zaka 33½ za moyo Wake. Ndiko kulondola. Taganizani za zimenezo. Ife taziwona izo ndi maso athu. Ife taziwona izo zikuchitika. Ife tinaziwona izo zitaloseredwa, nkubwera podzachitika, tazipenya izo. Opunduka, akhungu, mbuu, onyololoka, zinthu zoloseredwa zimachitika chimodzimidzi pa dontho. Sizinalephere konse. M’bale, izo ziyenera kutiyika ife mu kuchitapo ndi kudzichepetsa ndi kulemekeza.

160 Kuchokera kutali mmbuyo mu nthawi za Baibulo pamene Lawi la Moto linkapachikika pamwamba pa Israeli, ndipo Ilo linapangidwa thupi ndipo linakhala pakati pathu... “Ine ndinabwera kuchokera kwa Mulungu ndipo ndikubwerera kwa Mulungu.” Paulo Woyera analiwona Ilo ndipo anagwa cha fufumimba. Mphunzitsi wamkulu monga Paulo, wophunzitsidwa pansi pa Gamaliele, anagudubuzika mu fumbi ndipo analira, “Ambuye, Ambuye, Ndinu Ndani? Ndine wokonzeka kupita.” Mwamuna wamkulu, chimene iye anali, sikolala; ndipo iye anadzichepetsa yekha, chifukwa iye anawona Lawi la Moto. Iye sitikungoliwona kokha Ilo ndi maso athu likusuntha pakati pathu, koma ife mpakana tiri nalo Ilo mwa sayansi. Izo ziyenera kutiyika ife mu kuchitapo.

161 Ife tikuliwona Ilo likuchita zinthu zomwezo zomwe Ilo linkachita kumbuyo uko. Ilo likuchitabe izo lero. Lonjezo la Atate. Mai, ndi chiyani chimenecho? Ilo labwera kuti lidzatsimikizire Mawu, kuti litsimikizire kuti Mawu ali chomwecho. Icho chiyenera kuwuyika Mpingo mu kuchitapo, kodi inu simukuganiza chomwecho?

162 Ndi awiri iye anaphimbira nkhope yake mu kulemekeza. Awiri iye anaphimbira mapazi ake, kudzichepetsa. Ndipo ndi awiri iye anapita mu ntchito. Kutali iye anapita, anayika izo mu kuchitapo.

163 Tsopano, ife tiyenera kuti tikhale mu kuchitapo mwa kulemekeza ku Mawu. Ife tiyenera kuti tiziwawuza anthu.

164 Zizindikiro za kudza Kwake zikuwonekera, paliponse ife tikuziwona izo zikukankhikira mu Mawu. Ife tikumva za Mzimu Woyera ukubwera kudzatiwuzwa ife zinthu zinazake zomwe zikukonzekera kuti zichitike.

165 Mosapitirira kuposa zaka makumi awiri zapitazo kuchokera mu nyumba yomweyi ino, Iwo unanena za Purezidenti Kennedy akubwera podzalowamo. Iwo unanena chimodzimodzi zomwe zikanati zidzachitike, kuti akazi ndi zina zotero adzamuyika munthu uyu mkati, ndipo chimodzimodzi zomwe iye akanati adzakhale. Ndipo ife tinazidziwa izo nthawi yonse, ndipo anatiwuzwa chimodzimodzi basi zomwe zikanati zidzachitike. Ndipo pano izo ziri lero. Ndipo pano msonkhano uja ukubwera, Chitaganya cha Mpingo ndipo onse akubwera palimodzi. Nchifukwa chiyani izo sizikutiyika ife mu kuchitapo? Ndi kulondola. U nhu!

166 Mawu ndi mawu momwe Iye anayankhulira, izo zakwaniritsidwa pa ife pomwe. Izo ziyenera kutiyika ife mu kuchitapo.

167 Monga mneneri, ife tawona kubwera kunja kapena ku—kudza patsogolo kwa kuchokapo, kukanidwa, kudzikuza kwa zipembedzo, kutaya malo awo.

<sup>168</sup> Monga Yesaya anayima pamenepo, iye anali m—munthu wachipembedzo kuyamba ndi kuyamba. Iye ankatsamira pa mfumu, chifukwa iye anali munthu wabwino. Koma iye anawona chomwe kudzikweza kwa wekha kunamuchitira iye. Iko kunamuchotsapo iye kwa nthawi zonse. Ndipo ife tawona chomwe kudzikuzza kwa wekha kwa chipembedzo kwachita kwa mpingo. Iko kwawatengera otchedwa mpingo wachipembedzo kuchoka mu bwalo kwa nthawi zonse. Ndiwuzeni ine pamene umodzi unayamba wawukapo iwo utayamba wagwa. Kodi uli kuti iwo? Yang’anani mmbuyo kupyola mu mbirizakale ndipo muwone mpingo uliwonse umene unayamba wagwapo. Mwamsanga pamene iwo unachita bungwe, iwo unagwa, ndipo iwo sunabwerere konse kachiwiri. Uziya sanabwerere konse ku—ku kachisi kachiwiri. Iye anali wakhate masiku ake ena onse ndipo anakayikidwa ali wakhate. Inde, bwana!

<sup>169</sup> Tsopano, mneneri anawona chimene icho chinachita. Iye anawona kuti—chimene kudzikweza uko kunachita. “Bwanji, ife tiri. . .” kapena, “Pafupifupi yense. . . Palibe munthu angakhoze kubwera mu zipembedzo zathu kupatula izo zitatengera m—mayeso pamaso pa wazamisala kuti awone ngati ma I.Q ake ali abwino kapena ayi. Iye ayenera kuti akhale ndi D.D.D., Ph.D. asanati iye abwere komwe uko—kuyankhula ndi ife. Magulu athu sakanati akhale naye iye ngati iye sali wotero.” O, mai! “Opambana. . . unyinji wabwino mu dziko umabwera uko. . . Taonani pa magalimoto amene akhala mozungulira malo athu; iwo ndi ma Cadillac, ndi ma Rickenbacker, ndi zina zotero.”

<sup>170</sup> Ife tachiwona chinthu chimenecho chikufa. Ife tikuchiwona icho chitafa, ndipo chinthu chonsecho chakhala chodzaza ndi—ndi zoyikidwa—zapangidwa zironda—zironda zonunkha, kani, monga Baibulo limazitcha izo. Izo zonse ziri zironda palimodzi. Izo zikununkha. Ndiko kulondola. (Kuyankhula mwauzimu ine ndikunena izi. Mwaona?)

<sup>171</sup> Ife tawawona iwo akutaya kugwira kwawo pa—kugwira pa Mawu a Mulungu ndi kumakweza tizikhulupiriro. Kodi ife tikuchiwona izo zikuchita chiyani? Zikukanthidwa ndi khate, kusakhulupirira. Nha! Mai, o mai!

Monga Uziya anayesera kuti atenge malo a wodzozedwa wake—a udindo wodzozedwa atatha iye kukanthidwa, ndipo iye anapeza kuti analephera izo. Ndipo ife tayiwona mipingo iyi ikuyesera kutenga malo a udindo wodzozedwa kuti azilalikira Mawu a Mulungu ndi kukhala wophulitsidwa ndi icho. Iwo sali kudziwa choti nkuchita. Ukawayika Mawu pamaso pa iwo, iwo sadziwa choti achite. Ndi zoyipa. “Ife tikukhulupirira kuti izo zinali za tsiku lina.” Ndi chiyani chimenecho? Iwo asokonezeka. Iwe ungakhoze bwanji kutenga odindo wa wodzozedwa wa Mulungu ndi kumakana Mawu Ake odzozedwa omwe ali Mwiniwakeyo mu mawonekedwe a Mawu? Iwe

ungakhoze bwanji kukana kuti Mawu ali olondola ndiye komabe nkumanena kuti ndiwe wodzozedwa ndi Mzimu?

<sup>172</sup> Chinthu chokha chomwe chingawonetsere Mawu a Mulungu ndi Mzimu Woyera Iwowokha. “Pamene Iye Mzimu Woyera adzadza, Iye adzatenga zinthu za Ine izi ndi kuzisonyeza izo kwa inu.” Ndiko kulondola. Inu mungakhoze bwanji kutenga malo a udindo wa wodzozedwa ndi kukhala wa kachikhulupiriro kapena chipembedzo? Iwo ali akufa! Chinthu choti nkuchita ndi kugwera pansi ndi kufuula mokweza, “Ambuye Mulungu, ndine munthu wa milomo yosayera.” Inde, bwana!

<sup>173</sup> Zipembedzo zimenezo zikuyesa kutenga malo a mpingo woyera. “Ife timakhulupirira mwa Mulungu Atate, Wamphamvuzonse, Mlengi wa Kumwamba ndi dziko lapansi, ndi Yesu Khristu Mwana Wake. Ife timakhulupirira mu Mpingo Woyera wa Chiroma,” ndi zinthu zonse zosiyana izi. “Ife timakhulupirira mu kuyankhulana ndi oyera akufa.”

<sup>174</sup> Ine ndimakhulupirira mu kuyankhulana ndi Khristu. Inde, bwana! Ine ndikukhulupirira kuti oyera ali ku ulemerero, zedi. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti ife tiri ndi Mkhlapakati mmodzi pakati pa Mulungu ndi munthu. Inde, bwana! Bayani chinthu chimenecho... Pano, Baibulo likutsutsa zimenezo. Iwo amati, “Chabwino ilo ndi Baibulo.” Uyo ndi Mulungu! Mawu anali Mulungu, ndipo Mawu anapangidwa thupi ndipo anadzakhala pakati pathu. Tsopano, Mawu ali mu thupi lathu, kudzipangitsa Iwowokha kuwonetseredwa, odzozedwa ndi Mzimu Woyera. Nthawi yoti tipite mu kuchitapo. Ndiko kulondola.

<sup>175</sup> Zotsatira za masomphenya pa mneneri (o, mai!) anamupangitsa iye kuvomereza kuti iye anali wochimwa (mneneri wodzozedwa). Iye anati, “Ndine munthu wa milomo yosayera, ndine wolakwitsa. Ine ndachita zolakwika. Ndine wosayera inemwini.” Iye anali wochimwa. Iye anavomereza machimo ake. Inde, bwana! Zinapangitsa mneneri wa Mulungu kuti avomereze kuti iye anali wochimwa; ndicho chimene masomphenyawa anachita. Ma D.D.D., ena Ph.D. angaseke pa izo. Oyembekezeka kukhala ufumu winawake wolowezana wa mpingo wina.

<sup>176</sup> Kodi inu munamva zomwe Kadinolo wanena mu kuwonetsa kwa nkhani kuja lero? Iye anati, “Pali ena amene akuphunzitsa kuti kudza kwa Ambuye kuli kubwera posachedwa.” Iye akuti, “Koma zoon, ife tiyenera kuti tidzasiyane nalo gulu limenelo. Ife tikufuna kuti tigwirizanitse dziko la chipembedzo.” Chimodzimidzi basi. Anthu inu, musati mugone tulo tsopano. Zinthuzo zayandikira kuposa momwe inu mukuganizira. Munthu uyu ali pafupi ujayu yemwe sanali kumudziwa Yosefe, inu mukudziwa.

<sup>177</sup> Penyani, akubweramo mwandale basi monga izo zikanati zikhaliire. Iwo ali nako kugwira apa pomwe mu malo otsiriza awo, momwe iwo ati apange fano kwa icho pa kutenga Chitaganya cha Mpingo, ndi kulipangitsa ilo kumayankhula mofanana basi monga chirombo chinachitira, ndi kuchipatsa icho mphamvu kuti azizunza anthu onse aumulungu, ndipo chidzasintha nthawi ndi malamulo a Mulungu. Chimodzimodzi basi chimene icho chinanena. Ife tifika ku izo mtsogolo; tachedwa kwambiri usikuuno, koma ife titero—inukuzidziwa izo mulimonse. Inde, bwana!

<sup>178</sup> Iwo anampangitsa iye—anampangitsa iye kuti avomereze yekha kuti ali wochimwa...?...Bwanji, ngati izo zikanakhala otchedwa lerowa, iwo akanati, “Chabwino, ndine Dokotala *Wakuti-ndi-wakuti*.”

Ine ndinamumva bishopu akuti, “Pamene ine nditi ndikafike kumwamba, inu mukudziwa chomwe ine nditi ndikachite?” Anati, “Ine ndikapita kwa—kwa Yesu ndi kukati, ‘Inu mukudziwa yemwe ine ndiri? Ndine Bishopu *Wakuti-ndi-wakuti*.’”

Iye adzati, “Inde, Ine ndinawamva mayi anga akuyankhula za inu.”

Anati, “Anthu omwe amakhulupirira Baibulo ali monga oyenda kudutsa mu madzi a matope; iwe sumadziwa kumene iwe ukupita.”

<sup>179</sup> Musati muziganiza zimenezo. Iye ndiye Namulondolera wanga. (Ine ndikulalikira pa zimenezo mawa usiku.) Inde, bwana! Iye adzakulondolerani inu kupyola mu madzi onse amatope omwe alipo kuti mudutsemo, modikha mowopsya monse, ndi malo onse okwera, ndi malo otsika. Paliponse pamene pali, Iye adzandilondolera ine kuwoloka mtsinje wa imfa. Ameni! O, inde bwana! Iye adzandilondolera. “Pamene imfa idza ine sindidzawopa choyipa chirichonse pakuti Inu muli ndi ine. Inde, ngakhale ine ndiyenda kupyola mu chigwa cha mthunzi wa imfa, ine sindidzawopa choyipa chirichonse; Inu muli pamenepo.”

<sup>180</sup> “Ngati ine ndingakapange kama wanga mu hade,” Davide anati, “kumeneko Iye alipo.” “O, ngati ine nditadzatenga mapiko a mmawa, nkuwulukira kutali, kumeneko Iye alipo. Iye nthawizonse ali patsogolo panga, chotero ine sindidzasunthidwa.” Ameni! O, mai! Tengani mapiko amenewo ndipo pitani mu kuchitapo tsopano. Inde, bwana!

<sup>181</sup> Mneneri uyu anapita mu kuchitapo mwamsanga ndithu; iye anapita pa mawondo ake. Ndipo iye anati, “Ndine munthu wa milomo yosayera.” Ndiye mwamsanga pamene iye anavomereza, ndiye pakubwera kuyeretsa. Iwe uyenera kuvomereza choyamba.



182 Ine ndikufuna inu kuti muzindikire, pamene mneneri uyu . . . Taganizani za izo, a—osati . . . Munthu yemwe anayima ndi boma la feduro, mneneri wotsimikiziridwa, ndipo mwamsanga pamene iye anawona masomphenya oyamba amenewo . . . Iye anali asanayambe waonapo masomphenya kale; iye anali nazo mulimonse. Iye anali atamverera kutsogolera kwa Mulungu ndipo ankapita molingana ndi Mawu. Koma nthawi iyi anali masomphenya otseguka, ndipo iye anafuula, “Ndine munthu wa milomo yosayera ndipo ine—anthu onse awa ali osayera. Watsoka ndi ine, chifukwa ine ndikuwuona ulemerero wa Mulungu ukuwonetseredwa.” Ndipo ife timangoyang’ana pa iwo. Ife timayenera kuti tiziwulukira kutali. Mwaona, mukuwona?

183 “Ndine munthu wa milomo yosayera.” Iye anapita pansi pa guwa, ndipo iye anati, “Ndine munthu wa milomo yosayera, Ambuye. Kodi ine ndingakhoze kuchita chiyani, ine ndingakhoze kuchita chiyani, pakuti ine ndakuonani Inu mukuwonetseredwa pomwe pano? Ine ndikuwona Mngelo akugwedeza chinthucho. Ine ndinamuwona iye akuyankhula, ndipo chinachake chinasunthira kumbuyo patali.” Ameni! (Ine ndikuyembekeza kuti inu simukugona.) O, mai! Kuyankhula ndipo chinachake chinachitika. Ulemerero! Nchiyani chinachitika?

184 Ndiye ife tikupeza kuti iye anavomereza machimo ake, ndipo basi mwamsanga pamene iye anachita izo, liwu lalikulu ili lomwe linakhala likuyankhula linawulukira pansi, linatenga dzanja lake, linatenga mbaniro, linanyamula khala, analiyika ilo pa dzanja lake, anabwera kudzaliyika pa milomo ya Yesaya, ndipo anamuyeretisa iye.

185 Zindikirani, iye sanamutumize konse iye kuti apite akatenge digrii ya Ph.D. Iye sanamupatsa konse iye bukhu la malangizo kuti aphunzire; koma Iye—Mulungu anali akumusonyeza mneneri kuti mphamvu Yake yoyeretsa inali mwa moto wa pa guwa. Ameni! Mphamvu ya Mulungu yoyeretsa lero si kubwereza kachikhulupiriro kapena kujowina mpingo; ndi mphamvu ya Mzimu Woyera ndi moto umene umabwera pansi ndi kumuyeretisa munthu ku kusakhulupirira kwake konse. Ameni!

186 Njira ya Mulungu yoyeretsa mneneri ndi mwa moto, osati mwa tizikhulupiriro. Mneneri ankadziwa chiyani za tizikhulupiriro? Iye akhala akugwiritsidwa ntchito ndi Mulungu. Mawu anali oti azikakwaniritsidwa kupyolera mwa iye, chotero Iye sakanakhoza kumupatsa iye kachikhulupiriro. Iye akanati azigwiritsa ku kachikhulupiriro kameneko. Chotero Iye anatenga moto kuchokera pa guwa ndipo anamuyeretisa mneneriyo.

187 Kuvomereza choyamba, kenako kuyeretisa ndi moto. Ulemerero kwa Mulungu! O, penyani! Kuvomereza, choyamba, kuyeretisa, chachiwiri, kutumidwa, chachitatu. Ameni! Ndi

zimenezotu. Poyamba kuvomereza, “Ine ndalakwitsa!” Chachiwiri, kuyeretsa. Kulungamitsidwa, Kuyeretsedwa, ndi Ubatizo wa Mzimu Woyera. Mwaona? Kuvomereza, kuyeretsa, kutumidwa. “Pitani inu mu dziko lonse ndi kukalalikira Uthenga. Zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akhulupirira.” Amen!

<sup>188</sup> Pambuyo pa kuvomereza pamabwera kuyeretsa. Pambuyo pa kuyeretsa pamabwera kutumidwa. Kalalikireni Uthenga, kachizeni odwala. Ziribe kanthu chomwe anthu ankanena iye...

<sup>189</sup> Potsiriza mneneri wamng’ono wofunika uyo anafa pansu pa kuzunzidwa pa kukhala atachekedwa nthuli nthuli ndi macheke.

<sup>190</sup> Kumbukirani, zinali pamene Yesaya anapanga kuvomereza kwake kuti iye anali kulakwitsa. Iye anali palimodzi mu zonse wolakwa; iye anakhala akutsamira pa kachikhulupiriro kake (mwaona?), kutsamira pa—munthu, chinthu chopangidwa ndi munthu. Iye ankamuwona mfumu yemwe anali munthu wamkulu; iye anali munthu wachipembedzo. Koma iye anawona kuti anthu onse adzalephera. Mwaona? Koma pamene iye anasintho izo, ndipo nayang’ana mmwamba apo, ndipo nawona masomphenya Yemwe Mulungu anali, ndiye iye anati, “Ine ndikufuna kuvomereza ndine wolakwa. Tizikhulupiriro takale sitigwira ntchito panonso, chifukwa ito tafa kale ndipo talephera. (Mwaona?) Izo zakanthidwa ndi khate, koma ine ndawuona ulemerero wa Mulungu uli kukwaniritsidwa.” Kachikhulupiriro sikangakhoze kukwaniritsa zimenezo. Kachikhulupiriro sikangakhoze kunena izo mwanjira imeneyo. Kachikhulupiriro sikangakhoze kuchita izo mwanjira imeneyo. Izo zimatengera Khristu kuti achite izo mwa njira imeneyo. Ndipo mwamsanga pamene iye anawona izo, iye anati, “Tsopano, ine ndakhala palimodzi mu zonse wolakwa, Ambuye.” Ndiyeno panadza kuyeretsa; kenako panadza kutumidwa. O, mai!

<sup>191</sup> Panali pamenepo pamene Yesaya woyeretsedwa... Pamene Mulungu anayitana, “Ndani ati andipitire Ine,” ndipo anali Yesaya yemwe anati, “Ambuye, ndine ndiri pano; nditumeni ine!” Mneneri woyeretsedwa.

<sup>192</sup> O, kodi inu simukuwona *kukopa*? Musati mutenge kukopa kwa Marthela. (Ine ndikuyembekeza limenelo si dzina mkati muno.) Musati mutenge maina a—a—kukopa kwa msungwana wina wamng’ono yemwe amapita ku sukulu yapamwamba ndi inu, kapena sukulu wamba, kapena woyandikana naye wakhomo lina yemwe amadula tsitsi lake ndi kuvala akabudula; musati mutengere kukopa kumeneko. Musati mutengere kukopa kwa m’busa wina watizikhulupiriro yemwe angakane Mawu a Mulungu ndi kukupatsani inu kachikhulupiriro; musati mutengere kukopa kumeneko. Koma imani pamenepo mpaka

inu mutawona ulemereero wa Mulungu ukugwa, kuwona chinachake chikusuntha mwa mphamvu zake, ndi kuchiwona icho chikuchitika basi mwanjira yomwe Mulungu ananenera izo. Ndiye fuulani, “Watsoka ndi ine, Ambuye; ine ndakhala wolakwitsa. Ndiyeretseni ine tsopano, Ambuye. Ndiyeretseni ine! Mzimu wa Mulungu Wamoyo ugwe mwatsopano pa ine.”

Pamene khala la moto linamukhudza mneneri,  
Kumupanga iye wangwiro monga wangwiro  
akanakhalira;

Pamene liwu la Mulungu linati, “Ndati ati  
atipitire ife?”

Ndiye iye anayankha, “Ambuye, ine ndiri  
pano; nditumeni ine!” (Iye anali wokonzeka.  
Iye anali atawona chinachake. Inde, bwana!)

Mamilioni tsopano mu tchimo ndi manyazi  
akufa;

Mvetserani ku kulira kwawo kwachisoni ndi  
kowawa.

Fulumirani, m'bale, fulumirani ku  
kuwapulumutsa kwawo;

Mwamsanga yankhani, “Mbuye, ine ndiri  
pano!”

<sup>193</sup> Chinachake chiyenera kuti chichitidwe. Ndi mochedwa kuposa momwe ife tikuganizira kuti izo ziri. Mulole masomphenya a Mulungu awakope anthu chotero, kuti iwo akhoze kuwona kuti Mulungu yemwe uja yemwe anali mu kachisi ndi Yesaya ali Mulungu yemweyo mu malo Ake oyera lero. Iye ali mu malo oyera a Mzimu Woyera. Iye ndiye Mzimu Woyera. Iye kamodzi anali thupi; tsopano Iye ali Mzimu ukusuntha pakati pa anthu Ake, akudzisonyeza Iyeyekha wamoyo, osati chikhulupiriro chakufa, koma Khristu wamoyo, yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse. O, Yesaya, anayankha mofulumira, “Ambuye, pano; nditumeni ine.”

Tiyeni ife tipemphere. Ndi mitu yathu yoweramitsidwa . . .

Pamene khala la moto linamukhudza mneneri,  
Kumupanga iye wangwiro monga wangwiro  
akanakhalira;

Pamene liwu la Mulungu linati, “Ndati ati  
atipitire ife?”

Ndiye iye anayankha, “Ine ndiri pano;  
nditumeni ine!” (Palimodzi.)

Yankhulani, Ambuye wanga; Yankhulani,  
Ambuye wanga.

Yankhulani, ndipo ine ndifulumira kuti  
ndikuyankheni Inu.

Yankhulani, Ambuye wanga; Yankhulani,  
Ambuye wanga.

Yankhulani, ndipo ine ndiyankha, “Ambuye  
nditumeni ine!”

<sup>194</sup> Tsopano, izo zikhoza kukhala woyandikana naye wanu; izo zikhoza kukhala mkazi yemwe inu mumagwira naye ntchito, mwamuna yemwe inu mumagwira naye ntchito, koma alipo . . .

Mamilioni tsopano mu tchimo ndi manyazi  
akufa; (Mu tizikhulupiro ndi zipembedzo.)

O, mvetserani ku kulira kwawo kwachisoni ndi  
kowawa.

Fulumirani, m'bale, fulumirani ku  
kuwapulumutsa kwawo;

Mwamsanga yankhani, “Ambuye, ine ndiri  
pano!”

Yankhulani, Ambuye wanga; Yankhulani,  
Ambuye wanga. (Ine ndinaziwona  
masomphenya ochokera kwa Ambuye; ine  
ndinawona izo zikuchitika.)

Yankhulani, ndipo ine ndikhala wofulumira  
kuti ndikuyankheni (Iye wayankhula kale  
tsopano.)

Yankhulani, Ambuye wanga; Yankhulani,  
Ambuye wanga.

Yankhulani, ndipo ine ndiyankha, “Ambuye,  
nditumeni ine!”

<sup>195</sup> Tsopano, ndi mitu yanu yoweramitsidwa, ine ndikudabwa usikuuno, monga ine ndinakuwuzani ine ndikubwera kuno, kuti ine ndayesa kuti ndiwerenge chinachake chimene ine ndikuganiza kuti chikanakuthandizani inu. Inu munamuwona mneneri uja; iye anali mwamuna wamkulu. Iye anabadwa kwa cholinga choti akhale mneneri. Iye anapeza kuti iye anali atatenga njira yolakwika; iye anali akutsamira pa nkono wa Uziya, mfumu. Iye anawona kuti iwe sungakhoze kutsamira pa mikono ya thupi. Iyo ndi yokhoza kutha. Ndi kulakwa. Koma yang'ana mmwamba ndipo umuwone Mulungu atakhala pamwamba pa mpandowachifumu Wake. Yang'ana m'mwamba apo pa Yesu; Iye anati, “Ndine yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse.” Mulole Iye akunyamule iwe mu Mzimu. Penyani ndi kuwona ngati Iye sali yemweyo dzulo . . .

<sup>196</sup> Pamene Yesaya wamng'ono uyo anawona masomphenya a Mulungu akusunthira pansu ndi kulowa mu kachisi ameneyo, iye anali wokonzeka kuti avomereze zolakwa zake. Iye anali wokonzeka kuti avomereze kuti iye sanachite chinthu chirichonse cholondola. Ndipo kodi iye anawulukira ku fuko pamenepo; kodi iye anachita chirichonse chimene chinali cholondola ndiye. Chirichonse chimene iye akanakhoza kuchita, mpaka potsiriza iye anasindikiza umboni wake ndi magazi ake.

197 Ine ndikuganiza kuti uko kukanakhala kumverera kwa tonse a ife. Ndi angati akumverera kuti inu mukanafuna kuti munene—kumumva Mulungu akunena—kuti inu mukanafuna—mukanati munene kwa Mulungu, “Ine, ndiri pano; nditumeni ine!” Kwezani manja anu. “Ine ndiri pano, ndiroleni ine ndichitire umboni kwa bambo wa mkaka. Ndiroleni ine ndichitire umboni kwa—kwa aliyense yemwe ine ndingakhoze, kuchita chinachake. Ndiroleni ine ndichite chinachake. Ambuye, ine sindiri—kupempha kuti ndikhale mlaliki. Ine sindikupempha kuti ndikhale ichi, koma, Ambuye, ngati ndiri mchikumbe, ndipangeni ine mchikumbe yemwe angakhoze kuchitira umboni kwa mchikumbe woyandikana nane. Ndiroleni ine ndikhale mchikumbe kuti pamene ine nditi ndigulitse mbewu zanga, ine ndikhoza kuchitira umboni kwa ogulitsa mbewu. Ndiroleni ine ndikhale mchikumbe. Ngati ine ndiri—ngati ine ndiri mkazi, ndiroleni ine ndichitire umboni kwa bambo wa inshulansi. Ndiroleni ine ndichitire umboni kwa bambo wa mkaka, kwa mnyamata wa nyuzi. Ndiroleni ine ndichite chinachake, Ambuye. Ndiroleni ine ndipite mwa oyandikana nawo ndi kukapeza mwayi ndi mlongo wanga apa wakhomo linalo yemwe ali woyipa ndi wolakwa. Ndiroleni ine ndimupatse iye umboni ndi kukoma. Ndiroleni ine ndiphimbe nkhope yanga ndi mapiko anga a kudzichepetsa; ndiroleni ine ndiphimbe mapazi anga chimodzimidzi. Ndiroleni ine ndikhale wolemekeza mu Kukhalapo Kwanu, koma nditumeni ine ndi mapiko awiri enawo, Ambuye, mwamsanga kwa winawake, ‘Ine ndiri pano; nditumeni ine, nditumeni ine!’”

198 Mwa ulemu uwu tiyeni tonse tiyime ndiye tidzipangire tokha ntchito yodzipereka kwa Mulungu. Wamphamvuzonse ali pano. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Ife tiri mu Kukhalapo Kwake Kwauzimu. Musati muyiwale zimenezo tsopano. Kukhalapo Kwake kuli pomwe pano basi monga iko kunaliri. . . Moona, ine chiyimireni changa pano, ine ndawona masomphenya anayi kapena asanu kale akuchitika. Ndiko kulondola. Ndiko kulondola. Pakhala pali anthu awiri kapena atatu omwe ali pa mpingo pano omwe sananene kanthu; koma Iwo ali pano chimodzimidzi basi. Chabwino.

Tsopano, chimene ife tikufuna kuti tichite, mmodzi aliyense wa inu mwa njira yanu yomwe, tiyeni tidzipereke tokha kwa Mulungu.

Ife tikuwona chizindikiro chikuwonekera cha kudza Kwake kodala;  
 Yang’anani ndi kuwona, masamba a mkuyu tsopano akukhala obiriwira.  
 Uthenga wa Ufumu wapita ku fuko lililonse,  
 Ndipo ife tayandikira; mapeto akukhoza kuwoneka. (Ndiko kulondola. Ndi kulondola kumeneko?)

Ndiye mokondwera; ife tikalengeza Uthenga  
wa kuwonekera Kwake kodala;  
Posachedwa Iye akubwera mu ulemerero  
tikamuwuze mmodzi ndi onse.

Ndiye galamukani, inu oyera a Ambuye,  
Bwanji mukugona pamene mapeto  
akuyandikira,  
Tiyeni tikhale okonzekera kuyitana  
kotsirizako. (Ameni!)

Mafuko ali kusweka; Israeli ali kuwuka; (Iye  
ali fuko tsopano.)

Zizindikiro zomwe aneneri ananeneratu,  
Masiku a Amitundu akwanira,  
Ndi zowopsya zitachuluka, (Inu mukuziwona  
izo zikubwera kutsidya, osati mafuko okha,  
koma mipingo.)

Bwererani, O omwazika, kwanu.

Tsiku la Chiwombolo layandikira;  
Mitima ya amuna ikulephera mwa mantha.  
Dzazidwani ndi Mzimu Wake,  
Nyali zanu konzani ziwale;  
Yang'anani mmwamba, chiombolo chanu  
chayandikira.

Aneneri onyenga akunama;  
Choonadi cha Mulungu akuchikana,  
Kuti Yesu, Khristu, ndi Mulungu wathu. (Inu  
mukudziwa iwo akutero.)

Ndipo—koma ife tiyenda pamene Atumwi  
anaponda.

Pakuti tsiku la chiwombolo layandikira;  
Mitima ya amuna ikulephera mwa mantha;  
Dzazidwani ndi Mzimu,  
Nyali zanu konzani ziwale;  
Yang'anani mmwamba, chiombolo chanu  
chayandikira.

<sup>199</sup> Pukutani utsi wa chipembedzo uchoke. Pukutani mwaye  
wa chidziko uwo uchoke. Magazi a Yesu Khristu ali oposa  
kukwanira kuti akuyeretseni inu. Yang'anani mmwamba! Lolani  
nyali zanu zikhale zikuyaka. Tengani mapiko amenewo ndipo  
wulukirani kwa winawake pomwe pano.

Tiyeni tikweze manja athu tsopano ndi kunena, “Mulungu,  
ine ndiri pano; nditumeni ine.”

<sup>200</sup> Atate Akumwamba, ndikudzipatulira ndekha kwa Inu  
usikuuno, Ambuye, ndi mpingo uwu, utatha uthenga uwu,  
wamphamvu, wolimba, “Ine ndiri pano, Ambuye; nditumeni  
ine.” Pano pali mpingo wanga, Ambuye. Mulole iwo aphimbe  
nkhope zawo ndi kulemekeza. Mulole iwo aphimbe mapazi

awo mwa kudzichepetsa. Mulole iwo akhale ndi kulimbika kuti awuluke ndi Uthenga, mwamsanga, kwa winawake. Perekani izo, Ambuye. Mulole iwo akachitire umboni ndi kukoma, akakhale mchere wa dziko lapansi ndi Mpulumutsi wake momwemo. Ambuye Mulungu, iyi ndi nsembe yathu. Ichi ndi chopereka chathu. Uku ndi kupereka kwathu kuthokoza. Ichi ndi chomwe ife tikuchiyembekezera, Ambuye. Titumeni ife usikuuno kwa winawake yemwe ali wotayika. Mulole ife tikawakokere iwo ku mpingo mawa kwinakwake. Mulole ife tiwaphunzitse iwo njira ya Ambuye. Mulole iwo akhoze kupulumutsidwa, Ambuye, pakuti ili mochedwa kuposa momwe ife tikuganzira. Perekani izo, Ambuye.

<sup>201</sup> Mulole ife titanthauze izi mu mitima yathu. Ndipo pamene ife tikuyankhula izi, Ambuye, tengani khala la moto wa Mzimu Woyera kuchokera pa guwa pa Kalvare; khudzani mtima uliwonse ndi mlomo usikuuno, Ambuye, kuti ife tisamanene bodza ayi, kuti ife tizina Zoon. Titengeni ife usikuuno, Ambuye, basi chomwe ife tiri. Tonse a ife sindife alaliki. Tonse a ife sindife aneneri. Tonse a ife sindife oyankhula ndi malirime. Tonse a ife sindife ochita zozizwitsa; koma tonse ife tiri nacho chinachake choti tichite. Tisonyezeni ife kumene icho chiri, Ambuye. Kuchitira umboni, kuyimba mayamiko Anu. Ndipo monga mkate pa madzi, iwo udzabwerera tsiku lina laulemerero. Perekani izo, Ambuye. Ife tiri pano. Titumizeni ife kwa oyandikana nawo kulikonse kumene ife tingakhoze, kwa anthu anzathu, ndi kuwauza iwo za kudza kwa Ambuye. Perekani izo, Atate.

<sup>202</sup> Tidalitseni ife tsopano. Mulole ife tikakhale nako kupumula kwabwino mu matupi athu usikuuno. Mulole ife tikawuke ndi kubwera ku tchalitchi mamawa; ndipo mulole Inu mukayankhule chomwecho—mwamphamvu kwambiri mawa, kuti Inu musadzasiye mwala umodzi wosatembenezidwa, kuti mwamuna aliyense adzadziwe momwe angalowere mu izi. Tiphunzitseni ife, Ambuye. Ife tikuyembekezera. Mudzatiphunzitse ife mamawa momwe ife tingabwerere ku muyezo wathunthu uwu pomwe ife tingakhoze kukhala ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Ife tikuyembekezera pa Inu, Ambuye, ndi khala la moto lokonzeka kuti liyikidwe pa milomo yathu. Ife tikuyembekezera, Atate, mu Dzina la Yesu.

<sup>203</sup> Tsopano, ndi mitu yathu yoweramitsidwa. Ine ndiwafunsa abusa ndiye kuti abwere kutsogolo ku ntchito yobalalitsa. Mulungu akudalitseni inu. Ndikuyembekeza kuti ndidzakuwonani inu mamawa tsopano. Mulungu akhale ndi inu, chiritsani odwala onse ndi osautsika pakati pathu, kukupangani aliyense wa inu. . . ine ndikumverera kudzazidwa ndi Mzimu pakali pano. Ine ndikumverera Mzimu Woyera. Ine ndikumverera Kukhalapo Kwake. Ine ndikudziwa Iye ali pano. Ine ndikutsimikiza Iye ali pano. Ine ndikumuwona Iye;

ine ndikudziwa Iye ali pano. Ine ndamuwona Iye akusuntha, Lawi la Moto lalikulu lija. Ulemerero!...?...kuwonetseredwa kwa Umunthu Wake, umulungu wa Kukhalapo Kwake...?... Umunthu Wake wopambana. Mulungu, fungatirani pamwamba pa anthu awa; musalole kuti mmodzi wa iwo atayike, ine ndikupemphera. Ulemerero kwa Mulungu!





*KUKOPA KWA WINA* CHA62-1013  
(The Influence Of Another)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham wolalikidwa mu Chingelezi pa Loweruka usiku, Okotobala 13, 1962, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mchaka cha 1998 ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©1998 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)